ZIPHUNZITSO ZA CHI-SDA ZINASINTHIDWA

# M'MISONKHANO NDI MA-EVANJELIKO

## (ZOKHUZA MA-ADVENTIST OKHA)

- Kusintha mwa mphamvu, modabwitsa, kofulumira ndi kotheratu kwa ziphunzitso za mpingo wathu. Chochititsa mantha kwambiri ndi chakuti kusinthaku kunachitidwa ndi amuna awiri.
- Mbiri yofufuzidwa ndikulembedwa bwino yoyambira 1941 mpaka 2008.
- Nkhani yomvetsa chisoni ndi yochititsa mantha mu mbiri ya mpingo wathu.
- Mpfundo mazanamazana ndiponso maumboni ochokera kuzolembera zina ziripo
- Za momwe mwamuna m'modzi, wosakhalanso wa mpingo wathu anakhala akutsogolera za kusintha ziphunzitso zathu kwa zaka 34 komwe kwadzetsa chisokonekero cha muyaya
- Chinachitika chiyani ndi kutheka bwanji kuti ziphunzitso zachikhalire za mpingo wathu zisinthidwe
- Zalembedwa'zi zachokera m'maumboni a iwo anaziona zikuchitika, ku zolembera zina, mitu 70, ndi zoonjezera magawo anai zomwe mungazipeze m'bukhu lathu "Kusokonezedwa Kwathu ndi Ma – Evanjeliko [Our Evangelical Earthuquake.]" Onani tsamba 16. Mukuwerengachi ndi chifupikitso cha Bukhu'lo.

## ZOMWE ZINACHITIKA ISANAYAMBE MISONKHANO ( 1941 -1954 )


A Unruh alemba kalata (1949) – Zonse zalembedwa m'munsi zinayambira pa November 28, 1949, pamene a Unruh analemba kalata, yowayamikira a Barnhouse za ulaliki wao wa pa wailesi, - chinthu chomwe chikudabwitsa ambiri kuti zinatheka bwanji. Ndipo poyankha kalatayo, a Barnhouse anati anali odadwa kwambiri kuti m'modzi wa anthu oukira, mbusa wa chi-Adventist, awayamikire za ulaliki wao umene unali wa Kulungamitsidwa mwa Chikhulupiriro.

A Martin Anauzidwa Kulemba Bukhu (1954) – A Walter Ralston Martin (1928-1989) omwe anali mkuru wa zotchinjiriza Chikhristu mu Bungwe la Zosindikiza Mabuku la Zondervan, anali m'modzi wa anthu amene amalemba zowerengawerenga kawirikawiri m'magazini ya a Barnhouse yotchedwa "Muyaya [Eternity]."

Mu nyengo ya mphukira ya 1955, pamene anali kuyang'anayang'ana m'zolembera za a Barhouse, a Martin anapeza makalata omwe analemba a Unruh.

A Branson Atamwalira Kale (1954) – A William H. Branson (1887-1961) omwe anakhalapo mtsogoleri wa Bungwe Lalikuru [General Conference] loyendetsa Mpingo wa S.D.A. ndipo a Reuben R. Figuhr (1954-1966) anachita kulowa m'malo mwao, akanakhala ali moyo pa nthawiyo, kusokoneza ziphunzitso komwe kunachitika kudzera m'misonkhano ndi a ma-Evanjeliko sikukanachitika.

Koma , panthawi'yi, m'1955, a Branson anali ataiwalika – ndipo a Figuhr (omwe anasankhidwa May 1954), komanso sanali katswiri pa ziphunzitso za mpingo, anali ndi chizolowezi chomasiyira ntchito yao anthu amene anawakhulupirira ngakhale akhale a maudindo ochepa.




**KUSOKONEZEDWA KWATHU NDI MA-EVANJELIKO**

**MISONKHANO NDI MA-EVANJELIKO NDI NDI KUOPSA KWAKE**

**KWA NTHAWI YOYAMBA NKHANI YONSE IFOTOKOZEDWA**

**PALIBE KUTETEZERA KWINA M'KACHISI**

Asankhidwa a Froom ndi a Anderson (1955) – A Leroy Edwin Froom anali katswiri pa zofufuzafufuza, mpingo wathu sunayambe wakhala ndi munthu wotere, pamene a Roy Allen Anderson, omwe anakhalapo mlaliki ndiponso mtsogoleri wa m'bungwe la abambo anasankhidwa kukhala omakambirana ndi a Walter Martin. Iye (Anderson) anawaitana a Walter E. Read, omwe pa nthawiyo anali Mlembi wa Bungwe Lalikuru [GC] la mpingo koma woona za m'zigawo, omwe sanalinso katswiri pa ziphunzitso zathu.

A Froom anayesera kuzembazemba kuti asatengeko mbali pa misonkhano imachitikayo chifukwa analibe chidziwitso chokwanira kuti nkutchinjiriza ziphunzitso zathu, koma Anderson anawakakamiza kuti adzikhalapo ndipo iwo anakhaladi m'modzi wa anthu amene anadzetsa kulolerana pa ziphunzitso zathu ndi zofuna za a Walter Martin.

Kubetchera kwakukuru kunachitika, ndipo a Froom ndi a Anderson anadzipereka ndi kupangitsa misonkhano imachitikayo komanso bukhu lotsatira zokambiranazo la a Martin kuti zipambane kwambiri.

Zipambano Zoyambirira za a Anderson za Kusintha Mpingo (1941, 1949) – Kuyambira pachiyambi a Anderson, anayala maziko akuti zokambirana zomwe zimachitidwa zitheke. Atangosankhidwa kukhala woyang'anira Bungwe la Abusa (Ministerial Association) m'1941, a Anderson anaonetsetsa kuti mabuku awiri a nyimbo, Khristu Mu Nyimbo ndi Nyimbo ndi Kayimbidwe Kake (Christ In Songs and Hymns and Tunes) omwe anthu athu (a chi-SDA) anawakondetsetsa kwa zaka zambiri achotsedwe.

M'1949, a R. A. Anderson, mothandizana ndi a Froom, anabweretsanso kusintha kwachiwiri koonekera kwambiri.

Kumapeto kwa zaka za m'ma 1940'zo m'modzi wa ophunzira Bukhu Lopatulika wotchuka kwambiri wa mipingo ya Mpanduko analemba kuti ma-Adventist "amaukana Umulungu wa Khristu." Wolembayu ananena ichi chifukwa cha mau onena za umulungu wa Khristu omwe iye anawawerenga m'bukhu la Kuphunzira Bukhu Lopatulika m'Mabanja [Bible Readings For the Home] momwe munalembedwa kuti Khristu anatenga "thupi la umunthu lathu la uchimo'li." Atamva choncho, pamene bukhu'li limasindikizidwanso kachiwiri, Anderson anachotsa mau'wo.

Mau osinthidwa'wo analembedwa m'bukhu la Bible Readings For the Home lomwe linasindikizidwanso m'chaka cha 1949. Koma chodabwitsa kwambiri chinali chakuti anthu athu sanaturukire za kusintha kwa mau'ko mpaka pamene a Anderson anachita kuulura okha.

Zalembedwa m'munsimu ndi momwe linali bukhu loyambirira lomwe linali lokhoza:

"M'thupi lake la umunthu, Khristu anatenga thupi lathu la uchimo'li… Uku ndi kutsutsana kotheratu ndi chiphunzitso chakuti Khristu anabadwa ndi thupi lopanda ufooko wa umunthu ndiponso chakuti anabadwa mwa mai wopanda tchimo, kotero n'chifukwa chake sanatengereko chifooko chiri chonse cha uchimo, chomwe chinalinso chifukwa chimene Iye sanachimwire, ganizo lomwe likumuonetsera Khristuyo kuti sanali wa dziko lapansi lakugwali komanso sanali woyenera kudzapulumutsa anthu amene anafunitsitsa chithandizo chake…"

Bukhu Lopatulika likuphunzitsa momveka bwino ndithu kuti Khristu sanalandira thupi la chilengedwe cha angelo (kapena lomwe Adam anali nalo asanachimwe), koma analandira la mbeu ya Abrahamu.

## MISONKHANO YA MIYEZI 18 (MARCH 1955 – AUGUST 1956)

Msonkhano Woyamba (March 1955) – Mu nthawi ya msonkhano uwu a Froom anachita kafukufuku ndi kulemba zomwe anapeza; ndipo a Anderson analimbikitsa a Froom'wo ndiponso ubale wao ndi a Martin ndi a Barnhouse.

Monga zinali zoona kuti kagulu ka ma-Adventist atatu'wa (Froom, Anderson, ndi Read) kanali kokwanira

kuimira mpingo wonse? Iwowatu sanaimire okhulupirira enieni omwe amadziwa bwino za mbiri ya zikhulupiriro zathu. Zinali zodabwitsa kwambiri kuti zaka zisanu kusinthaku kusanachitike, patsogolo pa khamu lalikuru linasonkhana'lo ku zokambirana za Msonkhano Waukuru wa [GC], a Read anatchinjiriza chiphunzitso cha thupi la uchimo la umunthu lomwe Khristu anadzitengera pa Mwini yekha. Chinthu chomwe chinadzetsa chitsitsimutso chachikuru m'maora 24 oyambirira a msonkhano'wo.

Pa nthawi iyi, a Froom anagwiritsa ntchito nzeru zao modzipereka, kuyambira maora a chigawo chakumadzulo kufikira dzuwa kulowa, kuchokera pongotha kukomana koyamba, nalemba phunziro lokwanira masamba 20, kuyankha mafunso pa ziphunzitso zoyambirira omwe a Martin anawandandalika pa pepala. Ndipo zinayankha a Froom'zo zinatumizidwa kwa a Martin.

Tsiku lachiwiri la msonkhano ndi losaiwalika. A Martin anabvomereza kuti iwo ndi amene sankamvetsetsa za chiphunzitso cha chi-Seventhday Adventist, naonetsa m'machitidwe ao kuti anagwirizana nacho. Chipambano cha kanthawi kochepachi chinalimbikitsa a Anderson ndi a Froom kuposa pachiyambi: naganiza, iwo kuti tsopano atembenuze ndi kugonjetsa kotheratu ma-Evanjeliko'wo!

A Barnhouse Alowererapo (August 1955) – A Martin anafuna kuti naonso a Barnhouse akhulupirire kuti ma-Adventist ndi akhristu osati oukira Khristu. M'misonkhano imene inakhala ikuchitikira m'nyumba mwa a Dr Barnhouse inathandizadi kuti iwonso ndi mwana wao wa mwamuna abvomerezenso kuti panali zambiri zomwe anazimvetsetsa molakwika.

Maulendo Onse a M'madera Osiyanasiyana Alipiridwa (1955) – Atsogoleri athu anaitana a Martin kudzalankhula ku Sukulu ya Ubusa ya chi-Adventist, kenaka nawatengera iwo kukalankhulanso ku mpingo wathu waukuru wa Takoma Park. Iwo analipira zonse zofunikira pa ulendo wa a Martin wa ku Loma Linda, kudzanso maulendo ao a m'chaka cha 1955 ozungulira dziko lonse lapansi.

Mpfundo Zitatu – Chodziwika bwino kuyambira pachiyambi chinali chakuti zibvute zitani a Martin anali ndi ziphunzitso zitatu zomwe sanalore ndi pang'ono pomwe kuzisintha pa moyo wao – zomwe atsogoleri athu pozibvomereza zinadzetsa chisokonekero chamyaya mu mpingo wa Seventh-day Adventist. Pa ziphunzitso zina panali kutsutsana kwa apo ndi apo, koma pa zitatuzi, zomwe ndi maziko a chiphunzitso cha mipingo ya Mpanduko ya makono, panakhazikika chikhulupiriro chonse cha a Martin. Kuli konse anapita a Martin analankhula motsutsana ndi ziphunzitso zitatu za chi-Adventist (zomwe iwo sanagwirizane nazo), nawauza ma-Adventist kuti azisinthe zomwe ndi zakuti:

1) Nsembe yakutetezera machimo ya mwazi wa Khristu sinathere pa mtanda koma ikupitirirabe.

2) Chipulumutso chimatheka pamene chisomo chimayendera limodzi ndi chifuniro cha lamulo.

3) Khristu anatenga thupi la umunthu la uchimo mwakukhala kwake m'mimba mwa Mariya.

Ziphunzitso zitatu'zi zafotokozedwa bwino chiri chonse pa zoonjezera ziri kumbuyo kwa traki'yi.

Poyankhapo pazofuna za a Martin'zo, atsogoleri athu anakubvomereza kusinthako kuti nsembe yokhululukira machimo ya mwazi wa Khristu inathera pa mtanda pa Gologotha. Iwo anabvomerezananso kuti Khristu sanatenge thupi la umunthu wathu la uchimo'li. Chikhalirecho pa zikhulupiriro izi kuyambira cha nsembe yakukhululukira machimo chomwe timati ikupitirirabe kuchitika kufikira nthawi yachimaliziro m'Kachisi wam'mwamba, ndiponso chakuti Khristu anatenga thupi la umunthu wathu la uchimo'li, ziri maziko pomwe pakhazikika chikhulupiriro chathu. Ndipo kusokoneza chiri chonse cha izi kunatanthauzanso kusintha zikhulupiriro zathu zina zonse kuphatikiza cha chooonadi za chipulumutso, chisomo, kumvera ndiponso umuyaya wa malamulo a Mulungu.

Ngati kudzipereka nsembe kwa Khristu kunathera pa Gologotha, ndiye kuti anthu onse tabadwa pambuyo'fe tinapulumutsidwa kale. Choncho palibe chifukwa choti tidzibvutika zakukonza makhalidwe athu mwatsopano. Ndiponso kuti ngati Khristu sanatenge thupi lathu la ufooko la umunthu'li koma la angelo, sanayenera Iye kukhala womvera ndipo kusachita tchimo kwake si chitsanzo chomwe ife tiyenera kuchitsanzira. Ziphunzitso amazifuna a Martin'zi ndi zolimbikitsa anthu kukhalabe moyo wa uchimo, chifukwa mkati mwake zikufotokoza kuti palibe munthu angakhale wosachimwa chifukwa tinabadwa auchimo. (Chiphunzitso chosokeretsa, chongopekachi, chikulandiridwa ndi anthu miyandamiyanda chifukwa chikuwalimbikitsa kuti ngakhale adzichimwira-chimwira, adzapulumutsidwa ali m'machimo mwao momwemo ndi kulowa kumwamba.)

Chiphunzitso cholakwikachi chikutsutsana ndi chiphunzitso cha uthenga wa angelo atatu chomwe chikulimbikitsa anthu kupereka ulemu ndi kupembedza Mulungu woona; komanso chikutsutsana ndi chiphunzitso chakuti chiweruzo chikuchitika pa nthawi imene munthu ali ndi moyo; chikutsutsananso ndi chija chakuti tituruke m'mipingo yomwe ikukana kumvera, kuchita ndi kusunga mau ndi malamulo a Mulungu; ndiponso chija chakuti chizindikilo cha chirombo chidzasindikizidwa pa anthu onse omwe akukana ziphunzitso za choonadi.

Mu Uthenga wa angelo atatu, chiri chonse cha ziphunzitso zitatuzi chimangika pakumvera malamulo a Mulungu, kukhala ndi chikhulupiriro kuti munthu alandire chisomo cha Khristu, chomwe chimapatsidwa kudzera m'chitsanzo cha moyo wakumvera wa Khristuyo, imfa yake yakudzipereka nsembe, ndiponso ntchito yake yakutetezera m'Kachisi wakumwamba kuchokera komweko amatipatsa mphamvu zosungira malamulo onse a Mulungu opezeka m'mabuku onse ouzilidwa ndi Mzimu wake.

A Froom ndi a Anderson pakulolera ziphunzitso za chi-Evanjeliko, anadzetsa kusintha komwe kukugwirizana ndi chiphunzitso chakuti kusunga Sabata la m'Bukhu Lopatulika nkosafunika!

Zoonjezera zomwe ziri kumapeto kwa traki iyi zifotokoza momveka bwino za choonadi cha ziphunzitso zathu.

## Njira zomwe a Froom ndi Anderson Anathandizira a Martin Kusintha Ziphunzitso Zathu

A Martin ndi anzao anafunitsitsa kuisokoneza ndi kuichotseratu ndondomeko yonse ya chipulumutso pogwiritsa ntchito ziphunzitso zao. Cholinga chao cheni-cheni chinali kuchotseratu za kumvera, kuchita ndi kusunga lamulo loyera la Mulungu Mlengi, yemwenso ali Woyera.

A Martin anadza ndi chikakamizo chakuti mau ena ndi ena kapena onse ofotokoza bwino za ziphunzitso za chi-Adventist, kapena ziphunzitso zina za izo zisinthidwe kapena kuchotsedweratu. Mwina ndi mwina anati mungosokonezedwa chifukwa zikatero kudzakhala kosabvuta kuzisintha zikhulupiriro zathu.

Ndipo izi zinachitikadi kuti m'zolembera zina mau amene mpingo wa SDA unawagwiritsa ntchito mwapadera m'ziphunzitso zake anamasulidwa m'chilankhulo wamba kapenanso chachikunja cha anthu ophunzira a mipingo ina. Njira zinai izi zinagwiritsidwa ntchito kukwaniritsa cholingachi: ziphunzitso za chi-Adventist zinalembedwanso m'mau osinthidwa; zina amangotenga mau apo ndi apo aumboni kuchokera m'zolembera za Mzimu Wachinenero; kenaka adani'wa analemba "chitsimikizo cha mgwirizano" chongopeka m'bukhu lao, Mafunso pa Chiphunzitso (Questions on Doctrine [QD]) kuti ma-Adventist ndi akhristu ngakhale amakhulupirira ziphunzitso zomwe onse sankazimvetsetsa; iwo anafotokoza mobwerezabwereza kuuza okhulupirira achi-Adventist kuti asadandaule pakuti palibe china chiri chonse chasinthidwamo m'ziphunzitso za chi-Adventist'zo.

A Froom anatsindika pa magulu a mau awiri za umunthu wa Khristu monga momwe mau'wo amagwiritsidwira ntchito m'mipingo ya Katolika ndi ma-Evanjeliko – wopanda ndi wolowa m'malo mwa. Ichi chinakondweretsa kwambiri a Martin ndi a Barnhouse, pokhala iwo onse a chikhulupiriro [cha-Calvinist] chokana kusunga malamulo.

Magulu a mau awiriwa, wopanda ndi wolowa m'malo mwa sakupezeka mu zolembera zoyambirira za bukhu la QD lomwe linatumizidwa kwa akonzi a Review [Bungwe losindikiza Mabuku la Chi-SDA].

Ziphunzitso za chi-Calvinist – Cholinga cha a Barnhouse ndi a Martin chinali kufuna kutembenuza ma-Adventist onse kuti tikhale a chi-Calvinist. Iwo anali ziwalo za chi-Calvinist/dispensational wing of Evangelicalism. "Calvinistic" - chiphunzitso chomwe chimati chipulumutso chinaikidwiratu kale munthu aliyense asanabadwe osati pa zomwe munthuyo akuchita. Pamene "Dispensational" ndi chiphunzitso chomwe chimati asanaphedwe Khristu pa Gologotha chipulumutso chinali pakumvera, kuchita ndi kusunga malamulo koma pambuyo pa imfa ya pa Gologotha chipulumutso chiri mwa chisomo.

A Barnhouse ankakhulupirira kuti Khristu anatenga umunthu wophatikizana mbali ziwiri – womwe sunali wofanana ndi uja wa Adamu-asanachimwe kapena wa Mariya! Kwa iwo umunthu wa Khristu unali chabe chikutiro cha kunja chophimba umulungu wakumwamba wa chikhalidwe chopanda tchimo ndi changwiro.

Wofunsa: "Iwo (atsogoleri a chi-Adventist), monga sakumaphunzitsa kuti Khristu anali ndi thupi ngati la Adamu asanachimwe, simukuziona choncho?"

Barnhouse: "Sindikuganiza choncho. Chiphunzitso chao n'chakuti Khristu anali Mulungu-munthu. Adamu analengedwa kuti atha kuchimwa. Yesu Khristu anali Mulungu-munthu kutanthauza kuti anali wosati n'kuchimwa.

Nanga zinatheka bwanji ife kuwalandira amuna aziphunzitso zolakwikawa?

Muli yankho mu Mkangano Waukuru [The Great Controversy] 260-262 lomwe likuonetsa poyera za kuipitsitsa kwa chiphunzitso cha chi-Calvinist'chi chakuti mbali yomwe munthu ali inasankhidwiratu kale munthuyo asanabadwe chomwe chiri kungofuna kuwasokoneza anthu kuti asakuone kufunika kwakusunga malamulo a Mulungu.

Momwe a Martin Anasinthira Ena a Mabukhu Athu – A Martin sanasiyira pa kusintha ziphunzitso zathu kokha, koma anaumiriza Bungwe Lalikuru (General Conference) kuti lichotseretu ena – kapena kuwalembanso mosintha – ena a mabuku athu!

A Martin sanangoumiriza kuti zolembedwa zina za m'mabuku athu zichotsedwe kokha ndi nyumba zathu zosindikiza mabuku, koma anayambitsa ganizo lakuti

mabuku omwe anali ndi zolembera zimene iye anatsutsana nazo asasindikizidwenso – pophapokhapo ngati ndime kapena mau zosabvomerezeka zitachotsedwa bukhu'lo lisanafike posindikizidwa.

Tsiku lina a Martin anadza ndi bokosi, bokosi leni leni, lodzala ndi mabuku ochokera ku nyumba zosindikiza mabuku za chi-Adventist nati, "Kodi mukudziwa kuti mpingo wanu ukuphunzitsa zinthu izi? 'Ukunka ukuchitirachitira molakwitsa kwambiri abale, taonani m'bokosi'li.' Ndipo iye analiika bokosi'lo pamwamba pa gome ndipo pafupifupi mabukhu okwanira mazana awiri anaturutsidwa ndi kuyalidwa pa gomepo. Atatsiriza kuwerenga mabuku anayalidwa pagomewo kwa masiku angapo bungwe lomwe limayendetsa za nkhaniyi, linati, 'tiyeneradi kuchitapo kanthu mosachedwetsa.' Anzathuwa achitapo mbali yao, ife tinailawa osachita ntchitoyo mokhulupirika.

A Martin ndi a Barnhouse poona kuti anachitacho chinawadzetsera chipambano, anakakamira pomwepo kotheratu. Mabuku makumi angapo a chi-Adventist anasinthidwa mosamalitsa, pamene enanso ochuruka analetsedwa kuti asasindikizidwenso.

Pofunitsitsa kukhala pa ubale ndi ma-Evangeliko, atsogoleri a mpingo wathu anapita chitsogolo kuchotsa mabuku achikalekale omwe ananenedwa kuti munali zolakwika.

Mokondwera a Martin analemba mu (Eternity, October 1956) kuti mabuku "osachepera 20 pa mabuku zana limodzi liri lonse" a chi-Adventitst omwe amasindikitsidwa pa nthawiyo anali obvomerezeka – ndipo ambiri otsalawo anayenera kusinthidwa kapena kusasindikizidwanso mpaka kalekale.

(M'zolembera zao a Vance Ferrell akupereka mndandanda wa mabuku 100 a chi-Adventist, ambiri a iwo okhuza kwambiri za chiphunzitso chathu, kuti sakupezekanso pano.)

A Martin anauza atsogoleri anthu kuti m'malo mwake adzisindikiza mabukhu osiyanasiyana. Izi zikucitikadi, taonani, ndi mabuku a chiphunzitso cha mtundu wanji ali pakati pathu lero?

Mabuku onyoza a Ellen White. Mabuku a chiphunzitso chachikunja za "ungwiro." Mabuku okweza mipingo ya Mpanduko. Mabuku odzala ndi machenjerero otsogolera anthu kuti asamvere, kusunga ndi kuchita malamulo a Mulungu. Mabuku olimbikitsa achinyamata athu za masewero a zisudzo ndi zoseketsaseketsa. Mabuku ongosangalala ndi chipambano cha "kubzala mipingo" koma ya anthu osatembenuka, okonda akuimba ng'omba ndi obvina ndiponso owomba m'manja, ndi kudzigwedezagwedeza mwamanyado m'mapemphero. Mabuku omwe akulimbikitsa zosunga malamulo a Mulungu mokhulupirika akunenedwa kuti ndi a Chi-farisi chakale chokakamira chilamulo.

Chinthu Chinanso Chimene a Martin Anachisintha – A Walter Martin anasinthanso machitidwe omwe timadziwika nao pa wailesi zathu. Pachiyambi, monganso imachitira mipingo ina, tinagwiritsa ntchito wailesi zoulutsira mau ndi za kanema wosatchula dzina la mpingo wathu.

Koma mu uphungu wao, a Martin anapereka mpfundo zingapo zomwe anati ma-Adventist anayenera kuzitsatira. Imodzi ya ndondomekozo inali yakuti a Mau a Mzimu Wachinenero [Voice of Prophecy] ndi a Chikhulupiriro cha Lero [Faith for Today] adzitchula mpingo womwe akuchokera.

Misonkhano Yapambuyo: Kumapeto kwa 1955, patadutsa zaka ziwiri za misonkhano yakathithi, mbali ziwiri'zi zinagwirizana kuti iri yonse isindikize bukhu lofotokoza zakuchotsa chitonzo cha ma-Adventist m'maganizo a ma-Evanjeliko.

A Barnhouse anakhutitsidwa ndi ma-Adventist kuti tsopano anali ma-Evanjeliko m'ziphunzitso zao zonse zokhuza chipulumutso. A Martin anawauzanso a Froom ndi a Anderson kuti Mipingo Yakukonzanso (ya chi-Calvinistic) inali mkati mwakusinkhasinkha mozama za kuulandira mpingo wa Seventh-day Adventist kuti tsopano unali umodzi wa iwo kudzera m'ziphunzitso zake zikuruzikuru zokhuza njira ya chipulumutso! M'May 1956, a Barnhouse anaonetsedwa zolembera zimene a Froom anazilemba akuti "zotsimikizira" kuti Mai White anakwezanso ziphunzitso chimodzimodzi zomwe a Froom ndi a Anderson analikuzikweza.

A Froom ndi a Anderson kwenikweni anawerenga zolembera za a Barnhouse zomwe mutu wake unali "Bombalaphulika" ("Bombshell") ndi zina zotsatira pa izi momwe a Barnhouse'wo analembamo zakusinthika maganizo kwao mwatsopano pokuwalandira ma-Advestist monga ma-Evanjeliko anzao patsogolo ngakhale pa zolembera'zo zisanasindikizidwe. Zolembera zina zogwirizana ndi za a Barnhouse'zi zinalembedwanso ndi a Martin mu Eternity yomwe inatsatira.

## ZOLEMBERA ZA NKHANI'YI M'MAMAGAZINI OSAKHALA A CHI – ADVENTIST (SEPTEMBER 1956 – JANUARY 1957)

Mau Oyamba – Nthawi zonse ngakhale pamachitika misonkhano ndi ma-Evanjeliko, anthu athu samauzidwa ndi pang'ono ponse.

M'August 1956, miyezi khumi, isanu ndi itatu ya misonkhano inatha. M'September a Barnhouse analemba m'magazini ya Eternity imodzi ya nkhani zitatu zokhuza misonkhano yao ndi ma-Adventist ndiponso zakusinthika kwao maganizo za ma-Adventist. Uku kunali "kuphulika kwa bomba koyamba."

M'November 1956 zolembera zina zinaturukanso m'magazini yotchedwa Chiyembekezo Chathu [Our Hope] ya chi-Evanjelikonso momwe mtsogoleri wina wosinthikanso maganizo anachitira ndemanga zakuti ma-Adventist tabvomerezedwa kukhala ma-Evangeliko. Koma zolembera zochititsa chidwi kwambiri zinali zimene zinalembedwa m'masamba angapo akutsogolo mu magazini yomweyo: zolemberazi zinali zochurukirapo ndipo zinalembedwa ndi a Walter R. Martin yemwe anafotokozamo kuti aliyense achite "mtendere" ndi ma-Adventist chifukwa chakubvomereza kwao ndi mtima wonse kusiyako zina za ziphunzitso zao zoyambirira zomwe zinali zolakwika.

Bungwe Lalikuru [GC] loyendetsa mpingo wa SDA linachita mantha kuti lilankhulepo kanthu ndipo linalibe choti nkunena – kulengeza ku mpingo wathu za nkhani yaikuru, yakufulumira kusintha zikhulupiriro mu mbiri ya mpingowu.

Nthawi yoyamba imene mpingo wa Seventh-day Adventist unadziwitsa ziwalo zake za zinthu zomwe zinakhala zikuchitika, munali m'December 1956 pamene mosamalitsitsa unalengeza kwa ogwira ntchito ake m'magazini ya Ministry.

Kuonjezera pa magazini ya Eternity, Our Hope inatsimikizika kuti inali magazini yokhayo ya Mpanduko (Chi-Protestant) yokhala ndi mauthenga ofunitsitsa za mgwirizano mu mkangano'wu. Zimene ife tapezapo zofotokoza za kugulitsidwa kwa ziphunzitso zathu zinali m'zolembera zinai za a Martin, chimodzi cha a Barnhouse ndi za m'bukhu la a Martin! M'zaka zambiri zikupitazi, atsogoleri athu akhala akuyesayesa mobwerezabwereza, kulumikizana ndi mipingo ndiponso zipembedzo zina m'misonkhano yokhazikitsa Mgwirizano umodzi, komanso kuti mpingo'wu ukhale pa ubale ndi mipingo ina, chinthu chomwe chikutheka mwachipambano pano.

Zolembera izi za a Barnhouse ndi a Martin za m'Eternity, pamodzi ndi zopezeka m'bukhu la a Martin, Choonadi za Ziphunzitso za a Seventh-day [The Truth about Seventh-day Adventism,] muli zinthu zinai:

1) Ma-Adventist analora kulumikizana ndi mipingo ina pofuna "umodzi ndi chiyanjano;"

2) Ziphunzitso zoyambirira za ma-Adventist zinalibe tanthauzo mkati mwake;

3) Ma-Adventist anafunitsitsa kusintha ziphunzitso zao;

4) Ziphunzitso zatsopano ndi zosiyana ndi zoyamba zomwe zimatengedwa ngati choonadi.

Pomwe kusinthaku kumachitika palibe



USIKU NDI USANA

wokhulupirira wamba mu mpingo wathu yemwe anayesetsa kufufuza kuti adziwe chomwe chimachitika.

Ngakhale kuti chibvomezi cha ziphunzitso zolakwika chaphulika, atsogoleri a mpingo wa Seventh-day Adventist ndiponso abusa sakunenapo kanthu za kusintha kuli konse, koma akungopitirirabe kuchita zinthu mwa chinsinsi.

Zolembera za Bombalaphulika (September 1956) – M'June 1956, ndinali m'chaka chachiwiri cha zaka zitatu ku Sukulu ya za Ubusa, pafupi ndi Likuru la Bungwe Lalikuru (GC) la mpingo wathu. Ena a aphunzitsi anakhala akutchulapo zakusiyana maganizo ndi anzao za nsembe yakupulumutsa ya mwazi wa Khristu, thupi la umunthu wathu la uchimo la Khristu, ndiponso zolakwika zomwe Ellen White analibe nazo ntchito pakunena za kukhazikitsidwa kwa zikhulupiriro zathu.

Panalibe ali yense, ndipo palibe aliyense anamvetsetsa, za kugudwa mofulumira kwa Eternity magazini ya September pakati pa banja la ophunzira za ubusa. Iyi inali nkhani yokhayo inali mkamwamkamwa mwathu monga ana a sukulu.

Umu ndimo analembedwera mau oyamba pa tsamba 4 la magazini imeneyi: "Mau otsogolera a zolembera za magazini ya mwezi uno akhala ngati bombalophulika…. Zolembera izi ziri mau oyamba a zolembera zina zitatu zomwe zidzakhala zikulembedwa ndi a Walter R. Martin m'mamagazini kwa miyezi itatu yotsatira…"

Pena pake m'magazini'yi panalembedwapo mau a Barnhouse onena zakuphulika kwa bomba'li.

Pakufotokoza kwao za misonkhano imachitikayo, a Barnhouse anati: "Poyamba kukambirana nao zinapezeka kuti ma-Adventist anakanitsitsa kotheratu ziphunzitso zina, zomwe zimatengedwa kuti ndi zao. Iwo anakanitsitsa mpfundo yomwe tinawauza kuti amalitenga Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri kukhala maziko a chipulumutso chao.

"Koma a Martin anapeza chimodzi cha zolembera zathu chomwe munalembedwa mobvomereza kuti Sabata ndi chimodzi cha maziko a chipulumutso chathu, ndipo anachionetsa kwa imodzi ya nthumwi zathu yomwe inakachionetsa kwa atsogoleri a Bungwe Lalikuru (GC), komwe anagwirizana kuti zolembedwazo zisinthidwe ndi

kukonzedwanso.

"Machitidwe a mtundu ngati umenewu anakhala akuchitika pa chiphunzitso cha kukhala munthu kwa Khristu. Atsogoleri'wa anawauza a Martin kuti izi zikuchitika chifukwa pakati pa ziwalo zao panali 'nkhakamira zosasinthika' omwe anangogwiritsitsabe kuti Yesu anabadwa m'thupi lauchimo."

Izi zinawatsimikizira a Barnhouse kuti, tsopano ma-Adventist azilandira ziphunzitso zatsopano zosinthidwazo, ndiponso abvomereza ziphunzitso zofanana ndi za chi-Calvinist!

A Barnhouse anapitiriza: "Tsopano pakuti ma-Adventist akukhulupirira kuti ntchito yakupulumutsa ya mwazi wa Khristu inathera pa mtanda, nkosabvuta kwa iwo kulandira ziphunzitso zina zonse za chi-Calvinism chamakono."

Ma-Calvinist amakhulupirira kuti timapulumutsidwa kotheratu popanda kuchitapo kanthu kena kalikonse kabwino kapena koipa m'moyo uno. Makhalidwe alibe ntchito pa chipulumutso.

A Froom ndi a Anderson anawerenga zomwe a Barnhouse analemba zotchedwa "Bombalaphulika'zi," chifukwa zinaonetsedwa kwa iwo zisanasindikizidwe. Ndiponso mau amene a Barnhouse anawalembamo akuti, 'nkhakamira zokanika' ndiponso zambiri zomwe zinalembedwamo zinali zochokera mkamwa mwa nthumwi zimene zimaimira GC ya mpingo wa Adventist.

Mogwirizana ndi zomwe a Martin analemba m'Eternity panalinso ena omwe analemba m'Eternity yotsatira.

A George Knight anati: "Palibe pamene tikupeza kuti atsogoleri a ma-Adventist anatsutsapo, zakuti zolembedwa'zi sizinaturuke mkamwa mwao – komanso a M. L. Andreasen m'Makalata ao ku Mipingo anatsimikizira kuti mau'wo analidi a atsogoleri ao.

"Molingana ndi a Barnhouse, atsogoleri a ma-Adventist anabvomereza za chiphunzitso chakuti Khristu anabadwa 'm'thupi lopanda tchimo' ngakhale ena a olemba ao mwa apo ndi apo akhala akulemba motsutsana ndi chimene mpingo wao wonse unachibvomereza. Iwo (atsogoleri'wo) anatsimikizira a bambo Martin kuti mu mpingo mwao muli ziwalo zina zomwe ndi 'nkhakamira zokanika.'"

A Barnhouse anafotokozanso kuti ma-Adventist asintha ndipo akukhulupirira kuti kusunga Sabata la m'Bukhu Lopatulika sikungampulumutse munthu. Pamenepa, ndiye kuti palibe bvuto ngati ife tingasunge lina liri lonse la Malamulo Khumi.

Kubwereranso ku zolembera za a Barnhouse za "Bombalaphulika," iwo anapitiriza kuti, "Nthawi yambiri ya zokambirana zathu zoyambirira inali pakuti titsimikizirane chimodzi chakuti ma-Adventist sakhulupirira kuti kusunga malamulo kuli mbali ya chipulumutso....tinati atiuze cheni cheni za ichi (chomwe kwa ife chinali chosabvomerezeka) kuti Malamulo Khumi adzisungidwa, koma kuti m'chipunzitso (ichi) mulibe mphotho iri yonse yomwe itengedwe monga dipo la chipulumutso....

"Za chipunzitso cha [chiweruzo chakufufuza mu mtima], kwa ine, ndi chosamveka, chosokoneza, ndipo chiri ganizo longodzionetsera mu mbiri ya chipembedzo!

"Mbali imene ma-Adventist ena anaitenga, titailingirira bwino ena'fe tapeza kuti ndi yachilendo. Ingathe kungokhala mbali ya gulu lalikuru la utsogoleri wosokonekera umene cholinga chake chinali kufuna kupeza njira zomwe ungathe kulamulira nao anthu amene ali pansi pake mosabvuta poganiza kuti mwina anthu'wo angathe kukhala ndi maganizo osiyana ndi otsutsana ndi a utsogoleri woikika'wo.

"(1) Momveka bwino, utsogoleri wa ma-Adventist ukubvomereza kuti zolembera za Ellen G. White...sizofanana mphamvu ndi Bukhu Lopatulika.

"(2) Iwo akukanitsitsa motsindika kuti kusunga Sabata si njira yolandira nayo chipulumutso.

"Akuti iwo sakhulupiriranso, zomwe ena a atsogoleri ao oyambirira anawaphunzitsa, kuti ntchito yakupulumutsa ya mwazi wa Yesu sinathere pa Gologotha koma kuti Iye akuichitabe m'chipinda chopatulikitsa kumwamba kuyambira 1844. Chiphunzitso ichi achikaniratu mwatchutchutchu...Izi zikusonyeza poyera kuti zina zotsalazo nazonso nchodziwikiratu kuti ndi zolakwika zomasulidwa molakwika komanso zongopeka kuchokera m'maganizo a munthu."

A Barnhouse anakanitsitsa za kufunikira kwa Malamulo Khumi, Sabata la m'Bukhu Lopatulika, utumiki wa Khristu m'Kachisi wakumwamba, ndiponso choonadi chakuti Khristu anatenga thupi la umunthu wathu la uchimo'li.

Iwo analemba: "Ife sitikukhulupirira kuti pali mphekesera ya ndime iri yonse yomwe ikuchitira umboni, ndipo tikukhulupirira kuti machitidwe ena ali onse obvomereza izi ndi abodza, opanda tanthauzo komanso osapindulitsa!"

Palibe kuphulika kwa bomba kuli konse komwe kumakonza zinthu. Koma kumaononga, kupha anthu, ndiponso kupundula ziwalo anthu a moyo. Bombalinaphulika'lo la a Martin ndi a Barnhouse cholinga chake kudali kuononga:

Linaononga maziko a ziphunzitso zathu zoyambirira; kupha miyoyo ya uzimu ya amuna ndi akazi powaphunzitsa iwo kuti angathe kupulumutsidwa ali chikhalire mu uchimo wakuswabe malamulo a Mulungu; komanso linakhumudwitsa kwambiri okhulupirira amene anayesetsa kukhala osagwedezeka pa ziphunzitso zathu zoyambazo.

Zolembera zochepa zomwe zimapezeka m'Eternity poyambirira sizinalandiridwe ndi gulu lalikuru la ma-Evanjeliko ndi mipingo ina ya Mpanduko.

Kunamizira "Nkhakamira zokanika" kuti ndizo zimakakamira ziphunzitso zotchedwa zosayenerazo chinali chinthu chosamveka chifukwa ndi atsogoleri a chi-Adventist omwewo amene amanka akuphunzitsa kuti Khristu anatenga thupi lathu la uchimo'li nakhala moyo wopanda tchimo (m'ndandanda wa atsogoleri 50 waperekedwa.)

Zolembera za a Martin mu Eternity ya October 1956 – Pano pali mau ofunikira mwapadera okhuza zomwe zalembedwa pamwambapa opezeka mu zolembera zoyambirira za a Martin m'Eternity:

"...m'malo ena ziphunzitso za chikhristu zachikale ndi...Ellen White sizikugwirizana; ..koma pa ziphunzitso zikuruzikuru ndi zofunikira kwambiri zotsogolera kuchipulumutso cha miyoyo ndiponso kukula m'moyo wa Khristu [Ellen White akugwirizana ndi ma-Evanjeliko]."

Zolembera za a Martin mu Eternity ya Nonvember 1956 – Pano tiyeni tionenso gawo lachiwiri la zolembera za magulu atatu za a Martin zopezeka m'Eternity magazine.

Kufotokoza mwachidule za zikhulupiriro za a Seventh-day Adventist kochokera m'zolembera zodalilika, kunatsatidwa chifukwa cha ndime zisanu zopezeka m'bukhu la QD zomwe zikukanitsitsa ziphunzitso zathu zoyambirira mwachitsanzo cha kupitiriza kutitetezera kwa Khristu kumwamba ndi cha thupi lake la umunthu la uchimo'li.

Kupitiriza apo a Martin ananena kuti ndi mabuku 20 okha pa 100 ali onse a chi-Adventist omwe anali obvomerezedwa kusindikizidwa malingana ndi ziphunzitso zomwe zirimo; komanso kuti atsogoleri a mpingo anali otangwanika kusintha kapena kuchotseratu mabuku ena onse! Ukutu kunali kuphulikanso kwina kwa bomba!

A Martin anatinso, "Pali zolembera zambiri zomwe zinali kusindikizidwa, zinanso zinali m'malo osungiramo mabuku m'nyumba za anthu [momwe munali ziphunzitso zosafunika] choncho zisamalidwe kuti zisafalikire ngati a Seventh-day Adventist akufuna kukhala pa mgwirizano ndi mipingo ina ndiponso kukhala ndi chithunzi chabwino chakuti ndi omvera pakunena za ziphunzitso zikuruzikuru za chikhristu...

"Ndi mabuku ochepera 20 pa 100 ali onse omwe pakali pano akusindikizidwa omwe abvomerezedwa kapena kuti ali ndi ziphunzitso zoona za chi-Seventh-day Adventist...."

"Chikakamizo chakusasindikiza zolembera kapena gawo la zomwe ndi zokaikitsa zimene panopa zakanidwa ndi mpingo wa Adventist chiyenera kudziwitsidwa kwa osindikiza mabuku onse a chikhristu.

A Martin anafotokozanso kuti ma-Adventist ambiri amene anathirira ndemanga pa bukhu la QD akuti sakumdziwa munthu amene analilemba. Kafukufuku wa zaka zaposachedwapa watsimikiza kuti ndi a Froom. A Martin akutsimikizira ganizo'li pakulemba, "A Dr. LeRoy E. Froom... polemba bukhu lao latsopano la chiphunzitso cha mau a Mulungu lomwe liyambe kugwiritsidwa ntchito koyambirira kwa 1957 akufotokoza momveka kuti mpingo wa Seventh-day Adventist unakana ziphunzitso zake zakale zomwe zinali zosinjirira...

"A Seventh-day akufuna kukonzanso zolakwika zonse...ndi kuyanjana ndi mipingo ina yomwenso iri ziwalo za thupi la Khristu."

A Martin anauzidwanso ndi a Froom ndiponso a Anderson kuti ndi Hiram Edson ndi "ma-Adventist oyambawo" amene ankakhulupirira kuti muli Kachisi m'mwamba!

Zolembera za a E. Schuyler za m'Chingelezi m'Chiyembekezo Chathu [Our Hope] 1956 – "Chi-SDA chakhala chikusintha kwa zaka khumi zapitazi, ndipo muli abale ambiri mwa Khristu omwe ali mkhola la chi-Adventist'lo.

Zolembera za magazini ya Nthawi [Time] ya December 1956 – Time magazine inalengeza kuti misonkhano imachitidwayo inali ya chipambano kotero kuti ma-Adventist akuti "pofika mwina nyengo ya mphukira[spring] ikudza'yi asindikiza ndi kulengeza –kumasulira kwatsopano kwa ziphunzitso zao."

Zolembera za a Martin m'Eternity ya January 1957 – munali mau akuti, "ndi 'ziwalo zoyambirira' za mpingo wa Adventist zomwe zinakhulupirira kuti zinali 'mpingo wotsala.'"

Koma Chibvumbulutso 12:17 likufotokoza momveka bwino za mpingo wotsala kuti ndi iwo okhawo amene akusunga malamulo a Mulungu. "...chiphunzitso cha mpingo wotsala chomwe chinayambitsidwa ndi ma-Adventist oyambawo... ndipo chikuphunzitsidwabe mu mpingo, ngakhale chimatanthauzidwa mosiyana... Ma-Adventist ali ndithu mbali (motsimikiza) ya 'mpingo wotsala'..."

Monga mukudziwa kuti mipingo yonse ikupanga mbali ya mpingo wotsala wa m'masiku otsiriza? Ichi ndicho cholinga chomwe zolembera ziri m'mwambazi zikuchifuna.

Zolembera za a Barnhouse m'Eternity ya November 1957 – M'zolembera izi a Barnhouse analengeza kuti bukhu la QD lasindikizidwa. (Bukhu la a Martin, The Truth About Seventh-day Adventism linali lisanasindikizidwe mpaka pambuyo pa zaka ziwiri, m'1960.)

"...bukhu la QD liri ulamuliro wa ziphunzitso zao...Liri mau akutsimikizira kuti iwo azikana zolembera za ma-Adventist omwe anali oukira ndi kutsutsana ndi utsogoleri

wao wobvomerezeka…

"M'kuganiza kwanga mkaziyu [Ellen White] anasoweka kuzama, kulondora bwino zinthu, ndiponso maphunziro a padera…

"Mwina awerengi athu angachione chobvuta kuwerenga masamba onse 720 a bukhu la chi-Adventist [QD] la tsopano'li, ndikadakondwera mukanagulanso, kuwerenga ndi kufalitsa bukhu la bambo a Martin [lomwe lidzakhala litasindikizidwa m'zaka ziwiri zikudza'zi]."

## ZOLEMBERA PA NKHANI'YI M'MAMAGAZINI A CHI-ADVENTIST (DECEMBER 1956-APRIL 1960)

Mau Oyamba ku zolembera magulu asanu ndi awiri – Chodabwitsa kwambiri, a Froom ndi a Anderson anakhala chete mpaka December 1956 pomwe anayamba kulemba za nkhaniyi m'zolembera zao zoyambirira zokhala m'magawo asanu ndi awiri zomwe zimasindikizidwa m'magazini ya Ministry yokhayo, yomwe imatumizidwa kwa abusa ndi atsogoleri a mpingo okha. M'magazini iyi a R.A. Anderson anatchulamo kwa nthawi yoyamba za kufotokozedwanso mwapadera kwa umunthu wa Khristu m'bukhu la Maphunziro a Bukhu Lopatulika m'Mabanja [Bible Readings] la m'mbuyomu m' 1949 (werengani chifupikitso cha bukhu loyambirira lomwe linali lokhoza pa tsamba 1 pamwambapa).

A Anderson analimbikitsanso za kufunikira kwa Zoonjezera [Appendix B] pomwe panalembedwa mau osokoneza akuti, "[Khristu Anatenga Thupi Lopanda Tchimo la Umunthu" (mau a Mzimu wa Chinenero omwe anasinthidwa ndi cholinga) monga analembedwera m'bukhu la QD lomwe analitenga ngati kuti linali lokhalo lodalirika. Kusinthidwaku kunachitidwanso mwachinsinsi m'Bukhu 7A Lomasulirira Malemba a Bukhu Lopatulika la Chi-Seventh-day Adventist [Seventh-day Adventist Bible Commentary, Vol. 7A] m'zaka zapambuyo. A Anderson'wo anakuchita kusinthako mosadziwitsa akonzi a Bukhu Lomasulira Bukhu Lopatulika'lo za kusinthidwa kwatsopano'ko!

Posinthapo a Anderson analembanso mau akuti, "Zolembedwa izi ziri chimodzimodzi monga zinalembedwa ndi Ellen White…ndipo mokhulupirika zikuimira maganizo a mdzakazi wa Ambuye'yo." Lomwe linali bodza leni leni. Ndipo pofuna kupewa mkwiyo wa anthu, patadutsa mwezi umodzi chichitikire ulendo wa a Martin, a Froom analembera a Figuhr, mtsogori wa GC: "Mau ena asinthidwako pang'ono kusiyana ndi momwe mumawadziwira poyamba…"

Zolembera za a Froom koyambirira kwa magazine ya Ministry December 1956 – Izi zinali zolembera zoyamba kusindikizidwa ndi mpingo wathu zofotokoza za misonkhano ya atsogoleri athu ndi ma-Evanjeliko.

Uthenga wa m'zolemberazo unali wakuti anthu ena akhala asakuphunzitsa choonadi cheni cheni za ntchito ya chitetezero. Pokhala kuti kunali kulemba ndi kufalitsa koyamba kochitidwa ndi General Conference – zolembera'zo zinalembedwa m'gulu la zochitika za tsiku ndi tsiku [Journal] zomwe kwambiri zimatumizidwa kwa abusa ndi atsogoleri okhaokha.

A Froom analembanso: "A khristu ena akukhulupiririrabe kuti ziphunzitso zathu zimati Khristu akupitiriza kupereka nsembe ina yotitetezera kumwamba kuonjezera pa imene anaitsiriza pa mtanda…

"Ma-Adventist, motsutsana ndi ichi, akukhulupirira motsimikiza kuti zonse zinathera pa mtanda pomwe-paja, ndipo palibenso nsembe ina koma ija anadzipereka kamodzi-kunthawi-zonse ya pa mtanda…

"Pambuyo pa nthawi ya chaka chimodzi kapena kuposera apo, mafunso okwana makumi asanu kapena makumi asanu ndi limodzi…anatumizidwa ku General Conference [kuchokera kwa abusa] omwe anafuna kumvetsetsa chomwe chinali chiphunzitso cheni cheni cha chi-Adventist…

"Palibe kusintha kuli konse komwe kwachitikapo koonjezera, kuchotsapo, kapena kuonjezapo pa ziphunzitso zathu… Mayankho awa akuimira kaganizidwe ka gulu lalikuru la alaliki, aphunzitsi, ndiponso alembi ndi oyang'anira ntchito athu…"

Zolembera za mau oyamba a Ministry (wolemba sakudziwika ) April 1957 – "…Iye[Khristu] anali ndi thupi lopanda uchimo ngati limene Adamu anali nalo asanachimwe m'Edeni…Iye anali munthu ndithu, komanso Mulungu wophimbidwa m'thupi."

Zolembera za mau oyamba a Ministry (wolemba sakudziwika) June 1957 – Magaziniyi inalengeza kuti bukhu la QD linatsala pang'ono kusindikizidwa (ngakhale kusindikizako kunachitika pambuyo pa miyezi inai). Zolembera izi zinali malo okhawo pomwe panafotokozedwanso za chiwerengero cha misonkhano yomwe inachitika ndi a Martin ndi/kapena a Barnhouse kuti anakomana nao (kakhumi ndi kasanu ndi kamodzi).

"…bukhu latsopano, QD, latha kwangotsala kuti lituruke… Mwa mabuku onse amene tasindikizapo, palibe limene lalembedwa mosamalitsa kuposa ili. Inali ntchito ya gulu, osati ya mlembi m'modzi [!]

Zolembera za Mai Cox m'Ministry ya December 1957 – Zolembera izi ndi zoyamba za zolembera ziwiri zomwe zinangotsatira pambuyo pakuturuka kwa bukhu la QD kuchokera kosindikizidwa. A Froom ndi a Anderson anakhala akuyendayenda uku ndi uku kuti apeze (alembi awiri osakhala a chi-SDA) kuti athandizire kubvomereza zolakwa zao'zo.

Mutu wa zolembera zomwe zinali m'Ministry iyi unali, "Khristu Wopanda Banga la Tchimo," chiphunzitso chomwe chinali chachilendo chifukwa chinayesetsa kuugawa umunthu wa Khristu pawiri.

"Pali anthu ena omvetsetsa omwe amakhulupirira kuti pamene Yesu anabadwa mwa Mariya nkutheka anatengerako makhalidwe a chifooko cha umunthu wa mai ake, omwe anali pa mtundu wonse wa anthu kuyambira pamene Adamu anachimwa…

"A mpingo wa Katolika… sangathe, ngakhale pang'ono kubvomereza kuti Khristu anabadwa mwa mkazi amene anali ndi thupi la uchimo.

"…a Mpanduko ena akubvomereza kuti mwa chilengedwe Mariya ayenera kuti anapatsako zina za ufoko wa umunthu wake kwa mwana wake…kapena kuti Khristu anatengerako ufoko wa umunthu kuchokera mwa Mariya, komwe kungakhale kukweza ntchito imene Mariya anaichita kapena kutsindika pa chinthu chomwe chingathe kukhala chosabvomerezeka ndi cha kunja kwa Malembo…"

Ndi chokondweretsa kwambiri kuti a Froom ndi a Anderson sanaperekepo umboni ndi umodzi wochokera ku zolembera za chi-Adventist wakuti wina wa ife anaphunzitsapo za chiphunzitso chachilendo ndi cholakwika'chi m'Ministry magazini iyi.

Zolembera za a W.G.T. Shedd m'Ministry ya 1957 – Tikubwera tsopano ku zolembera zachiwiri za chilendo m'Ministry ya December'yi.

Izi zikufotokoza kuti Khristu anali ndi umunthu wa thupi lopangidwa ndi magawo awiri omwe mkati mwake munali anthu ambiri osiyanasiyana, omwe anamchititsa Iye kukhala munthu wosiyana ndi anthu ena onse! A Shedd akuti chiphunzitso cha "chimunthu chopangidwa ndi anthu ambirichi" chinayamba ndi Akatolika.

Chiphunzitso cha Akatolika za Umunthu wa Khristu – Mau anasandulika thupi, osati munthu, koma mu umphumphu wa iye mwa mwini yekha, kuchokera momwe munaturuka chimunthu chopangidwa ndi anthu ambiri, chomwe chinali Mulungu-munthu.

"Chilengedwe ndi kupatulidwa kotheratu kwa thupi la umunthu kunali chinthu chofunika pa machitidwe oyenera ndi oulumikizanitsa umodzi wa thupi ndi Mau, yemwe…kuchokera m'chiyero chake cha umulungu sakanatha kudzidetsa mwini yekha podzitengera thupi la uchimo."

Zolembera za mau oyamba a m'Ministry ya March 1958 – Kenaka a Froom analandira madandaulo ochuruka pa zolembera zoyambazo, kuonjezera apo anthu anaganiza zopereka madandaulo otsatira'wo popanda kuikapo maina ao.

Zolembera za March'zi zinafotokoza kuti (onse!) "atsogoleri a mpingo 250" omwe analandira bukhu la QD anabvomereza kotheratu ndi kugwirizana kuti "pasakhale kusintha kuli konse pa zomwe zinalembedwa'zo." Kuchokera pamenepo, madandaulo a pansi pamtima ochokera kwa anthu osiyanasiyana anayamba kubwera mwaunyinji. Pochita mantha kuti anthu angatutumuke kwambiri za ziphunzitso zolakwika zomwe bukhu'li limaphunzitsa, bodza ili linakonzedwa, "Kubvomerezeka kwa bukhu'li kukuchokera ku zigawo zonse za mpingo



m'dziko lapansi" " ndiponso mogwirizana kotheratu ndi zolembera zomveka bwino za Mau a Mzimu Wachinenero."

Bodza, Bodza, lamkunkhuniza!

Zolembera za a Figuhr m'Review ya April 1960 – Kumapeto, patapita miyezi 43 kuchokera pomwe a Barnhoue analemba Bombalaphulika yomwe inadzidzimutsa mpingo wathu, ndiponso miyezi 30 kuchokera pomwe QD linaturuka kosindikizidwa – mau analembedwa kwa anthu athu kuti aliwerenge! Koma bukhu'lo sinatchulidwe ndi dzina lake kuti linali Mafunso pa Chiphunzitso [QD], koma anangonena za bukhu latsopano "lokondedwa" la a Martin.

## MU NTHAWI YAKUKONZEKERA *MAFUNSO PA CHIPHUNZITSO [QD]* (1956-1957)

Ogwira Ntchito ku Review Akhuzidwa Kwambiri – A Froom anali wotangwanika kulemba ndi kukonzakonzanso zolembera zoyambirira [manuscripts] za bukhu lomwe linali nkudza. Kupita chitsogolo ndi kubwerera m'mbuyo kwakuru kunachitika pa nthawi yakulemba QD kotero kuti akonzi a ku Review, yomwe inangoyang'anizana khomo ndi khonde la nyumba ya General Conference anakhuzidwa kwambiri. Mobwerezabwereza iwo anayesetsa kukonza mau omwe anasinthidwa, anachotsedwa, komanso onama omwe anali m'bukhu'lo; koma pobweranso zinakonzedwa'zo zimapezeka kuti zaikidwamonso. Chokonza

chokhacho chomwe sichinasinthidwe chinali mau akuti "nsembe ya chitetezero" m'malo mwa mau akuti "nsembe ya kupulumutsa yokhayo" inachitika pa mtanda.

Kusakaniza uku kwa choonadi ndi bodza kunapangitsa anthu ambiri omwe anawerenga mau'wa kusokonekera powatenga mau olakwika ngati okhoza ndi okhoza ngati olakwika.

A Francis D. Nichol analemba kalata kwa a Prezidenti a Figuhr kuwauza kuti mau ena amalembedwa anali akuti apite kwa a Martin kotero kuti "ambiri a ife, powalingirira mwakuya, sitikugwirizana nao."

Koma, mosafokera, ngakhale akonzi a ku Review anayesetsa kuchotsa zolakwika, a Froom ndi a Anderson anapitabe chitsogolo ndi cholinga chao.

A Raymond Cottrell, m'modzi wa othandizira akonzi a mabuku ku Review, analemba kalata kwa a L.E. Froom.

"…Paulo anafotokoza kuti cholinga cheni cheni cha ntchito ya kuyanjanitsa ndi nzeru ya chipulumutso ikuonekera mwa Mkuruwansembe wathu wakutumikira m'Kachisi wakumwamba…pamene m'malo ena m'bukhu la QD, pofotokoza za utumiki wa Khristu m'Kachisi, liu 'kutetezera' linachotsedwa.

"…inutu mosazindikira mwatsogoleredwa kulolera kusinthanitsa choonadi, kuti mudzichiphunzitsa mogwirizana komanso mokondweretsa mipingo yotchuka ya chi-Evanjeliko…

"Mutitsimikizire kuti palibe chotisokoneza kuchokera m'bukhu likunenedwa'li chomwe pambuyo pa zaka 50 zikudza'zo sichidzatitsamwitsa kutilowetsa ku chitaiko."

Pa October 2007 titangodutsa pang'ono zaka 50, ndipo zotsatira za m'QD zikuonekera ndi kupitiriza kufooketsa chilimbiko ndiponso kuononga khalidwe lathu lomvera Mulungu. M'modzi wa gulu la akonzi athu analemba, "Ndikukumbukira ngati kuti zachitika dzulo pamene akuluakulu atatu anagwirizana ndi kulembedwa kwa bukhu la Mafunso pa Chiphunzitso [QD], naletsa bungwe la akonzi a ku Review ndi Herald pa January 30, 1957, kuti 'asapezeke wokonzanso chiri chonse cha zolembera ziri m'bukhu'lo."

M'mawa umene'wo tinali m'Ofesi ya Mabuku Omasulira Bukhu Lopatulika, a Raymond Cottrell anaturuka m'chipindamo ndi chopukutira pa dzanja lao la manzere ndi mbale ya madzi…Ndipo ali yense wa ife ogwira ntchito ya Mabuku Omasulira Bukhu Lopatulika tinatsanzira posamba manja athu pa cholakwika china chiri chonse chokhuza kapena chinali m'bukhu la QD."

Pa January 23, 1957 nyumba yosindikiza mabuku ya Review and Herald inalandira zolembera [manuscripts] zomwe zinayenera kusindikizidwa "monga momwe zinaliri" kuti zisindikizidwe kukhala bukhu koma osakonzanso china chiri chonse cha zolemberazo.

Panalibe pena pali ponse, m'bukhu'lo, kapena nthawi ina iri yonse – pomwe mlembi wa QD anatchulidwa. Nthawi zonse zimangofotokozedwa kuti "gulu losankhidwa kuchokera pakati pa atsogoleri a chi-Seventh-day Adventist, aphunzitsi a Bukhu Lopatulika ndi akonzi a mabuku" ndiwo analemba bukhu'li. Chikhalirecho choonadi chake ali a Leroy Edwin Froom omwe analemba bukhu – lonse'lo.

A Andereasen Ayamba Kulemba Motsutsa – Kuyambira ndi pepala lomwe analilemba pa February 15, 1957, a M. L. Andreasen analemba mapepala ena motsatana odzudzula za chonyansa chinali nkuchitikacho. Mulungu amakondwera ndi amuna ndiponso akazi omwe adzaima nji ndi kuchitapo kanthu pamene zinthu zafika poipa, iwo amene adzachitchinjiriza choonadi chake pamene chikuponderezedwa ndi iwo ofuna kuchisintha chikhulupiriro mokomera nthawi yomwe alimo.

Kunali pamene a Andreasen anawerenga zolembera za a Barnhouse za 1956 zotchedwa Bombalaphulika, kuti anatsimikizika tsopano za choipa chomwe kweni kweni chinali kuchitika.

Iwo anakhumudwa kwambiri ndi zomwe analemba a Froom m'1957 zakuti "Kudzipereka nsembe kwa Khristu pa mtanda [kuli] kokwanira, kwangwiro ndi mapeto a ntchito yakutetezera machimo."

Chodziwika bwino kwa Andreasen chinali chakuti ntchito yakutetezera inali "m'magawo atatu."

Khristu anakhala moyo wangwiro ndi wosachimwa, umene anationetsera monga chitsanzo kuti ife tikhalenso chomwecho.

Imfa yake yakudzipereka mwini yekha nsembe pa mtanda

M'gawo lachitatu, Khristu anationetsera kuti munthu angathe kukhala woyera monga Iye ali woyera ndi thandizo lomwe Iye ali wokonzeka kulipereka. Gawo ili likuphatikiza kukwera kwake kumwamba ndi kukhala ku dzanja lamanja la Mulungu… Pano Iye akuyeretsa ndi kutsuka tchimo mwa oyera mtima ake pansi pano. Iyi ndi ntchito ya kutetezera yomwe akuichita m'Kachisi woona."

Ku "m'badwo wotsiriza uno" a Andreasen akuphunzitsa kuti Khristu ndiye chitsanzo cha momwe ophunzira ake angathe kukhalira ochirimika mwangwiro m'moyo uno. Momwe iwo angathere kukhala olakika ndi ogonjetsa m'zonse.

Pa March 11, 1957, a M' L. Andreasen analemba kalata yakukhuzidwa kwao kwa Prezidenti wa GC yakuti:

"Ngati bukhu ili [QD] lingasindikizidwe, padzakhala chisokonekero kufikira kutha kwa dziko lapansi, chifukwa maziko achikhulupiriro chathu adzachotsedwa."

"…Ngati wina angalore amuna awa kulemba kapena kulibvomereza bukhu'li kuti lisindikizidwe, ine ndikutsutsa…Ziri kwa inu kuubalalitsa mpingo kapena kuumanga pamodzi."

Pambuyo pa milungu iwiri analemba: "Zikundibvuta, sindingathe kungokhala chete, pamene mdani akuononga maziko" a ziphunzitso za kudzipereka nsembe yakutetezera tchimo m'Kachisi wa m'Mwamba ndi chiweruzo chakufufuza m'mitima.

"Kuchotsa ziphunzitso izi kuli chimodzimodzi kuthetsa chi-Adventist…

"Uku ndikupandukira kwakukuru kumene mpingo'wu sunayambe wakuchitapo."

Pa March 9, 1958, pambuyo pakuturuka Mafunso pa Chiphunzitso [QD] ku nyumba yosindikizira mabuku, a Andreasen anawalembera a Figuhr: "Ndikulilira anthu anga. Uku ndi kupandukira komwe kunalosseredwa kale…Ndikuyesetsa kupulumutsa mpingo wanga wa pamtima kuti usadzinyonge."

Kenaka a Andreasen analemba ndi kufalitsa ponse ponse mapepala asanu ndi anai pansi pa mutu umodzi wakuti, "Kuyanjanitsidwa ndi Mulungu" m'chaka cha 1957 ndi kumayambiriro a 1958. Awa anatsatidwa m'1959 ndi ena achiwiri omwe mutu wake unali, "Makalata ku Mipingo," omwe pambuyo pake anasindikizidwa m'kabukhu ka masamba 100 komwe mutu wake unali womwewo.

Bvuto lalikuru linali lakuti iwo anali okha omwe anaima nji pa choonadi pa nthawiyo! Pakanakhala kuti panali ma-Adventist 10,000 okhala ndi changu cha choonadi monga Andreason, mwina mwake mpingo ukanakhalabe uli m'ziphunzitso zolamitsa ndi zoyera zoyambazo.

## KUFALITSIDWA KWA *MAFUNSO PA CHIPHUNZITSO [QD]* (OCT. 1957)

Bukhu lomwe linausintha mpingo wa Seventh-day Adventist kotheratu – Kunali kumapeto kwa October 1957 pomwe Mafunso Pa Chiphunzitso linasindikizidwa. A Froom analemba ku Mau oyambirira a bukhu'lo kuti linali ndi ziphunzitso zathu zonse zobvomerezeka.

"Cholinga sichinali kuzisintha ziphunzitso koma kuzilemba m'chilankhulo chomwe chinali chopepuka ndi chomveka kwa onse okhuzidwa ndi za Mau a Mulungu…" "Sikunali kufuna kukhazikitsa ziphunzitso zatsopano za chikhulupiriro chathu…" "Mayankho opezeka m'bukhu'li anali kutambasula komveka bwino kwa ziphunzitso zathu…" "Palibe chiri chonse chomwe chasinthidwa ndi kusindikizidwa mogwirizana ndi zolakwika zomwe munthu m'modzi anazichita kapena maganizo a kagulu kochepa kanazibvomereza…" "Zolakwika zimene anthu pang'ono paokha anazichita ziyenera kukanidwa poyera…" "Tisamadziwike ndi kusalidwa chifukwa cha mau ena omwe ali osamveka bwino."

Kuyang'ana M'mbuyo Kuchisokonezo Chinachitidwacho – Mau onse ali m'munsi'wa analembedwa pambuyo pa zaka 50 bukhu loyamba la Mafunso Pa Chiphunzitso [QD] litasindikizidwa.

[QD] "likupereka chikaiko za tsogolo la zomwe ma-Adventist kweni-kweni amakhulupirira.." "ladzetsa za chilendo kwa anthu ena ndi ena za chomwe chiphunzitso cha mpingo chiri.." "laononga kwakukuru pobweretsa magawano m'malo mwa umodzi mu mbiri ya mpingo wa Seventh-day Adventist momwe magulu awiri adzakhala akulimbana mpaka kalekale.." "laika mkangano wosatha wa ziphunzitso za mau a Mulungu.." "bukhu losokoneza mu mbiri ya Seventh-day Adventist.." "kulembedwa ndi kuturutsidwa kwake kwadzetsa kusiyana maganizo ndi kupatukana.." "zambiri za ziphunzitso za m'bukhu'li zawagawa ma-Adventist kuti ena agwirebe ndikukhulupirira 'chi-Adventist chachikalekale ndi choyambacho motsutsana ndi gulu limene lasankha ziphunzitso za chi-Evanjeliko.." "lachigulitsa chi-Adventist ku chi-Evanjeliko.." "kulemba ndi kufalitsa [QD] kunali kulakwitsa kwakukuru.." "Ponyengedwa ndi ma-Evanjeliko m'ma 1950, atsogoleri a chi-Adventist anayambitsa chinthu chimene sanachiyembekezere m'pang'ono pomwe. Ziphunzitso zeni-zeni za chi-Adventist zinasinthidwa mofulumira ngati madzi othamanga kudutsa pamalo otsetsereka." "Ndikukhulupirira kuti kulowa m'zokambirana ndi ma-Evanjeliko ndi kulembedwa komanso kufalitsidwa kwa Mafunso pa Chiphunzitso kunadzetsa makhalidwe ochonganachongana, kukaikirana, kusakhulupiririrana, manong'onong'ono ndiponso kutaya chikhulupiriro mu utsogoleri."

M'modzi wa abusa okhuzidwa kwambiri analosera za choopsya chachikuru chomwe chinali kudzachitika kutsogolo pakunena 'chipasupasu chiri nkudza.'

A Froom anaonetsabe mtima wachipambano. Pambuyo pa zaka 14, mokondwera iwo analemba kuti ngakhale Akatolika analikonda QD. Naonjezeranso, ngakhale Mgwirizano wa Mipingo ya Dziko Lapansi [World Council of Churches] unalikondanso.

A Walter E. Read Apuma Ntchito (1958) – Panangodutsa chaka chimodzi kuchokera pomwe Mafunso pa Chiphunzitso linasindikizidwa, a W. E. Read anaganiza zopuma pa ntchito. Anthu ena akuganiza kuti anatopa kosaneneka ndi zomwe zimachitika ngakhale sanatenge gawo lalikuru m'misonkhano ndiponso kulembedwa kwa QD.

Kulifalitsa Bukhu'li Paliponse – Mafunso pa Chiphunzitso linasindikizidwa ndi mpingo wathu kumapeto kwa October 1957. Ndipo a Froom ndi a Anderson anakonzetsera

zakuti ligawidwe mothamanga ngati moto pa udzu wouma.

Patangodutsa mwezi umodzi QD litasindikizidwa, a Andreasen, pokhumudwa ndi zomwe anawerenga kuchokera m'bukhu'lo, analembera kalata a Prezidenti a Figuhr: "Ndakhumudwa ndi mtima wanga wonse, kukhumudwa kwakukuru…Umodzi wa mpingo ukuswedwa…Bukhu'li [QD] likanidwe ndi kuchotsedwa mofulumira, ngati tikufuna kupulumutsa mpingo."

Pa November 6, kalata yosainidwa ndi dzina la a abusa a Figuhr inatumizidwa kwa atsogoleri onse a zigawo za mpingo. Iye anawalimbikitsa iwo kugula chiwerengero chachukuru cha bukhu'lo m'magulu. Cholinga cha a Froom ndi a Anderson chinali kufuna kutontholetsa onse amene anawatsutsa. Atsogoleri ambiri a mpingo anachizindikira ichi, koma ngakhale anawerenga zolembera za Andreasen, anasankha kukhalabe mbali yolakwikayo.

A R. A. Anderson, omwe anali ndi chikoka chachikuru, anakonzanso zogawa mwa ulere zikwizikwi za bukhu'li ku masukulu onse a Ukachenjede ndi a Ubusa a Chikhristu m'dziko lonse lapansi.

Magazini ndi zolembera zina zonse za m'zigawo za chi-Adventist anafunsidwa kulengeza za bukhu'li. Zolembera zomwe sizinali za chi-Adventist anazifunsanso kutengako mbali yolengeza ndi kusindikiza zithunzithuzi za bukhu'li. Kabukhu kolengeza za malonda ka masamba-anai kanalembedwa ndi kugawidwa kwa abusa amene sanali a chi-Adventist. Atsogoleri otchuka m'zachipembedzo m' America wa Kumpoto anatumizidwa mabukhu a ulere. Mipingo inapemphedwa kukhala ndi chiwerengero chokwanira cha bukhu'li m'malo mwao mowerengera mabuku komanso kulipatsa mwa ulere kwa abusa a mipingo ya Mpanduko [chi-Protestant]. M'chaka cha 1970 a Froom anafotokoza kuti mabukhu oposa 138,000 anagawidwa.

Abusa a Theodore Carcich, omwe anali a Prezidenti a Chigawo cha Central Union, ndi mtsogoleri yekhayo yemwe anakanitsitsa kubvomereza chikakamizo cha kugawa bukhu'li. Iwo analemba: "Bambo a Martin akupitiriza kugwira ntchito yakusokoneza zikhulupiriro zathu mothamanga..chinthu chomwe makolo athu anachikana zaka za m'mbuyomu." "Mafunso pa Chiphunzitso ndi machenjerero ndiponso chinsinsi chakuyesetsa kupondereza maziko a ziphunzitso za chi-Seventh-day Adventist."

M'chaka cha 2006 a Herbert Dougless analemba: "M'1957, ndinakaonana ndi kulankhula zina ndi zina zokhuza ziphunzitso za Bukhu Lopatulika ndi a Arthur White.. Iwo anandiyankha, 'Herb, ndinaganiza kuti ndiyesetse kufotokoza malingaliro anga kwa a Froom ndi a Anderson.'

" A R.R. Figuhr…anakwanitsidwa ndi chomwe chinaoneka ngati chipambano choposa [ndi kusiyidwa kwakutchedwa kuti mpingo wa SDA uli kagulu kochita za chipembedzo mosinjirira [cult].

"Anthu ambiri akuganiza kuti ngati abusa a Branson (Prezidenti General Conference 1950-1954) sakanadwala , chinthu chomwe chinamkakamiza kuchotsa dzina lake pamaina omwe anaperekedwa kuchisankho cha Mtsogoleri wina wa Bungwe Lalikuru'li m'1954, Mafunso pa Chiphunzitso silikanapeza mpata wolembedwa..

"[Atsogoleri a mpingo] anawatsimikizira kuti kusiyana maganizo komwe kunalipo kunali chifukwa chakusiyana kwa kamveredwe ndi kamasulidwe ka mau. Ichi chinapusitsa antchito a mpingo nakhala mtulo ndi kusankha kukhala chete osachitapo kanthu."

A Froom ndi Anderson anautengetsa mpingo wa Seventh-day Adventist napambana! Anagonjetsa posintha, ndi kupondereza, ziphunzitso za okhulupirira oposa myanda umodzi a chi-Advent!

M'zaka za pakati pa 1957 ndi 1971, a L. E. Froom ndi a R. A. Anderson anatangwanika kwambiri. Maulendo mazanamazana omwe iwo amawapanga kunka akulankhula ku mbali zonse za dziko lapansi amalipiridwa kuchokera ku thumba la ndalama za General Conference.

Zosokoneza m'QD pa Umunthu wa Khristu – Mosachita kufunsa, kulakwitsa kochita zinthu akudziwa kunachitidwa m'zomwe a Froom analankhula ku misonkhano yao ndi ma-Evanjeliko ndiponso m'bukhu, Mafunso pa Chiphunzitso.

A George Knight akufotokoza kuti alembi a QD anawauza a Martin bodza kuti, "chiwerengero chachikuru cha mu mpingo kuyambira pachiyambi 'chakhala chikukhulupirira kuti thupi la umunthu la Khristu "linali lopanda uchimo.'"

Uku kunali kusemphanitsa choonadi! Ambiri a iwo ochedwa'wo "nkhakamira zokanika" anali atsogoleri a General Conference, a mipingo, akonzi a Review, alembi odziwika bwino, ndi aphunzitsi otchuka a m'masukulu a ukachenjede.

Mu kufufuza kwao kozama, a Ralph Larson sanapeze mlembi ndi m'modzi yemwe wa chi-Seventh-day Adventist amene analemba patsogolo pa 1952 yemwe anatsutsanapo ndi chiphunzitso chakuti Khristu anadzitengera pa Mwini yekha thupi lathu lakugwa ndi la uchimo'li. Ellen White sanakaike ndi pang'ono pomwe kunena kuti Khristu anadzitengera pa Iye mwini thupi lathu lakugwa ndi la uchimo.

A Froom anachita mayere kufuna kumva maganizo a atsogoleri a chi-Adventist, ndipo anapeza kuti 'pafupifupi onse' anabvomereza kuti Khristu anali ndi thupi lathu la uchimoli, ngakhale iwo [a Froomu'wo] anapitiriza ndi zachinyengo zao'zo.

Kuyesera Kubvundikira Chinyengo – Pamene anthu athu amauzidwa za kusintha komwe kunachitidwa mu ziphunzitso zathu, a Froom ndi a Martin anapezana ndi chitsutso osati chochokera kwa okhulupirira a chi-Adventist okha – komanso osakhala a chi-Adventist –omwenso amazindikira kuti chisokonezo china chake chimachitika! Kuti ziphunzitso za chi-Adventist zimasinthidwa!

A Anderson anawalembera a Martin: 'Zingatithandize pamodzi ndi okhuzidwa ena onse ngati titawauza anthu athu kuti azindikire kuti palibe kusintha kodetsa nkhawa kwa ziphunzitso zathu, koma maka kuti zikhale zomveka bwino."

Kunena za a Barnhouse, iwo amadziwa bwino lomwe kuti ziphunzitso za chi-Adventist zikusinthidwa, - ndipo anabvomerezanso ichi m'zolembera zao!

"Kwa ena'fe, zikuoneka kuti ziphunzitso za chi-Adventist zikusinthika kukhala zina zatsopano.."

M' Our Hope munalembedwa: "Chi-Adventism chakhala chikusinthika."

Mu 2004 a Ralph Larson analemba: "Iwo [a Froom ndi owathandizira ao] anabweretsa chinyego chambali ziwiri. Anatsimikizira ma-Calvinist kuti ife tasintha ziphunzitso zathu, ndipo pa nthawi yokhayokhayo kuwatsimikiziranso ma-Adventist kuti sitinasinthe.. Chochitika choterochi sichinali mwangozi. Chinali chochitidwa mozindikira ndiponso ndi cholinga cha chinyengo.

Atsogoleri Ena Achi-Evanjeliko Aturukira za Chinyengochi – Atsogoleri ena a chi-Evangjeliko anachiturukira chinyengochi kudzera muzolankhula za pawiripawiri za a Froom ndi a Anderson.

A M. E. DeHaan analemba: "Bukhu ili lakhazikitsidwa m'chilankhulo cha pawiripawiri ndiponso kudzitsutsa kosaneneka."

Norman Douty anafotokoza kuti a Barnhouse ndi a Martin "anapezeka mu zokambiranazi kuchokera ku zolankhula zomwe zimanenedwa kwa iwo ndi ma-Adventist eni ake."

Otsutsa a chi-Evanjeliko angapo anatsindika kunena kuti panalibe msonkhano wa Bungwe la General Conference uli wonse womwe anabvomereza Mafunso pa Chiphunzitso, choncho bukhu'li linali lobvomerezeka koma osati mwa chilongosoko.

A Harold Lindsell a ku Sukulu ya ukachenjede ya Fuller Theological Seminary, ananena momveka bwino kuti, "Alembi a QD sangathe ndiponso sakulankhula ndi ulamuliro.."

Iye anaonjezera kuti ngati ziphunzitso za chi-Adventist zokhuza nthawi yakumapeto [za zochitika m'masiku otsiriza] ndi Chihema zitachotsedwa, kudzakhalanso kutha kwa mpingo wa chi-Adventist! "Kungochotsa izi..pomwepo padzakhala popanda maziko olimba akuti chi-Adventist chikhazikikepo."

A Frank A. Laurence analosera kuti bukhu la a Martin'li lidzadzetsa chisokonekero ndiponso "mkwiyo"… "Ili ndi bukhu lomwe lidzakhala likumangozungulira pakati pa ma-Evanjeliko ndi ma-Adventist kufikira Baptist ya kumwera idzasankha kazembe woimira ku Vatican."

Kupsetsa Mtima kwa a Barnhouse – Mu zolembera zao, Bombalaphulika m'Eternity (1956), anthu amene anakhalabe mosagwedezeka m'chikhulupiriro chochokera m'Bukhu Lopatulika kumayambiriro a mbiri ya mpingo wathu ananyozedwa ndi kalankhulidwe ka chipongwe ka a Dr Barnhouse.

A George Knight akufotokoza kuti, "Alembi ena anamfotokoza Dr Barnhouse kuti anali 'wotengeka,' 'wopanda mantha ndi wamwano,' yemwe anali wokonzeka kutsutsa momwe 'angafunire.' Kalankhulidwe kamphamvu ndi kobwerezabwereza koyambanitsa-nthawi zonse ka a Barnhouse mosakaika konse kanachita kwakukuru ndi kubweretsa magawano.

"Iwo analemba kuti Mafunso pa Chiphunzitso 'ndikatanthauzidwe ka mau komwe kachepetsa mphamvu ya zolembera za ma-Adventist omwe anagalukira ndi kulemba motsutsana ndi utsogoleri wao woikika,'…'utsogoleri wanzeru womwe walimba mtima kutsutsana ndi ziwalo zake zonse zomwe zinafuna kukhala ndi machitidwe osiyana ndi omwe utsogoleri wa nzeru [kutanthauza wa a Froom] wa mpingo'wo wakhazikitsa.'

"Ndi zoonekeratu kuti a Barnhouse eni ake anachita kwakukuru kuyambitsa mikangano pakati pa ma-Adventist."

## ZOKAMBIRANA PAKATI PA A HUDSON NDI A BARNHOUSE

Munthu woyamba kusindikizanso zolembera za a Andreasen anali a Al Hudson, msindikizi wa zolembalemba m'Baker, Oregon.

Iye analemba: "Ogwira ntchito a ku General Conference akuonetsera poyera kuti…kumbali yaikuru ataya masomphenya auzimu..

" Tikufuna tifotokoze maganizo athu momveka bwino kuti tikulitenga bukhu, Mafunso pa Chiphunzitso kukhala ngati mwana wobadwira m'chigololo cha uzimu.

Pa May 16, 1958 a Hudson anawatumizira a Donald Barnhouse uthenga wa pa lamya. Ichi chinachitika chaka chimodzi ndi theka pambuyo pongotsiriza kulembedwa kwa "Bombalaphulika" m' Eternity ndiponso nthawi yochepera chaka chimodzi pambuyo pongoturutsidwa QD. Mau amene analankhula a Barnhouse m'kukambirana kwa pa lamya'ko anali a phwasulo.

Iwo anafotokoza kuti atsogoleri a SDA

anakanitsitsa zina za ziphunzitso zao zoyambirira…Iye anachidziwa ichi, anatero, ndiponso atsogoleri eni ake'wo anachitsimikiziranso ichi.

A Barnhouse sanangouzidwa kokha ndi a Froom ndiponso a Anderson kuti iwo monga atsogoleri anali kukanitsitsa ziphunzitso "zolakwika" za ma-Adventist oyambirira – komanso kuti ziwalo zonse za mpingo wa Adventist zinagwirizana nao kwatunthu za kukanitsitsa ziphunzitso'zo! A Barnhouse anaonetsa mkwiyo wao pa mbali zonse ziwiri pa ma-Adventist eni ake komanso pa zikhulupiriro zao.

M'zokambirana izi "(H)" akuimira a Hudson akulankhula ndi "(B)" a Barnhouse akulankhula. Izi ndi zochepetsetsa zotengedwa kuchokera ku zokambirana zazitali za pakati pa awiriwo:

"(B) M'mapemphera mpingo uti? (H) Ndine wa Seventh-day Adventist…Pali chinthu chimodzi chimene ndifuna kumvetsetsa kuchokera kwa inu…Kodi atsogoleri a Seventh-day Adventist anakuuzani kuti anabvomerezedwa ndi ali yense kapena sanafunse ali yense za kuti akufuna kukhala pa chiyanjano ndi Mgwirzano [National Association) wa ma-Evanjeliko?

"(B) Sindikuganiza kuti pali chikaiko chiri chonse kuti a Seventha-day Adventist, maka atsogoleri ao , akuchiona kukhala chofunikira kweni kweni kuti adzipempha kwa ali yense pofuna kukhala monga ma-Evanjeliko. Ndinanena kuti 'Chomwe ine ndikunena ndichakuti ma-Adventist ndi akhristu.' Ndikukhulupirirabe kuti ziphunzitso zao ndi zokhotakhota kusiyana ndi za gulu lina liri lonse la chikhristu m'dziko lapansi. Ichi ndikutsimikizira mosakaika konse. Mwachitsanzo, chiphunzitso cha chiweruzo chakufufuza mumtima ndi chonyansitsitsa, chongodziyenereza chomwe sichinayambe chaphunzitsidwapo.. Chabwino, tiyeni tilankhule motere, komanso m'njira yabwinoko, atsogoleri amene alemba bukhu'li [QD] anasiya kukhulupirira ziphunzitso za gulu loyambirira la chi-SDA.. Ngati mukufuna kuonetsadi kuti muli ndi choonadi, chitani cholemba ndipo mubwere poyera ndi kufotokoza motere, 'Tikufuna tibvomereze poyera kuti tiri ndi zolakwika m'ziphunzitso zathu zoyambirira. Tifuna kuzisiya izi ndi kupita chitsogolo ndi choonadi cheni cheni.'

"(H) Kunena mosabisa, pali kusiyana kwakukuru pa zomwe inu mukulemba ndi kufalitsa ndi zomwe atsogoleri athu amatiuza. Pano ndikungoyesetsa kumva kwa inu ngati ife tasinthadi."

"(B) Chiri chonse chimene ndachilemba chimakhala chitawerengedwa kaye ndi atsogoleri a Seventh-day Adventist ndisanachifalitse. Palibe mzera ndi umodzi womwe wa mau umene ndaulemba womwe sunawerengedwa ndi a Froom… Panopa ndikukalalikira ku mpingo wa Sevent-day Adventist ku Takoma Park, Washington. Tinali ndi a Dr. Roy Anderson omwe anadzaima pa gome lathu kulalikira ku mpingo wathu wa chi-Presbetare….

"Tamvani ndikuuzeni, ngati simukufuna, ndikutanthauza ngati mungayesere kulemba bukhu kapena china chiri chonse chomwe simungapezeke kusinthidwa kwa chi-Adventist, tiyenera tikutcheni monga timachitira mbuyo'mu, 'Okana-Khristu.' Apo ndiye kuti ndiyenera ndilembenso ku dziko lonse za kusintha maganizo kwanga, ndi kutumiza



zolembedwazo ku alembi a Time Magazini, ndi kunena, 'Zomwe Munalemba' – kodi mudawerenga izi pamene zinaturuka m'Time? Pomwepo, nditalembera ku magazini ya Time'ko ndidzafalitsanso m'Eternity ndi kupepesa ku Talbot for King's Business, Moody Monthly [onse maina a mamagazini], ndi kuti, 'Ndinalakwitsa. Anthu awa akadali otsutsanabe ndi Khristu. Mupitirizebe kuwawerengera limodzi ndi Amboni za Yehova omwe alinso ngati iwo.

"(H) Inu makamaka mukukhulupirira, ndithu, kuti bukhu lathu, Mafunso pa Chiphunzitso, likugwirizana ndi zomwe mwalemba mu magazini yanu ya Eternity…"

"(B) …bukhu [QD] likufotokozadi chimodzimodzi, mwachitsanzo, timtenge munthu aliyense amene akunena kuti ndikofunikira kusunga Saturday ngati tikufuna kupulumutsidwa, kutero nkulakwa. Bukhu lanu likutero." "Mumakukhulupirira kuti Sunday ndi chizindikilo cha chirombo, sichoncho?...

"…ngati mukukhulupirira kuti kusunga tsiku liri lonse kupatula Saturday ndi chizindilkilo cha chirombo ndiye kuti muli kumbali ya anthu okana-Khristu chifukwa mukukana chipulumutso chakuchitidwa mwa chisomo.

".. chiphunzitso chotero osachita kufunsa, ndi chochokera kwa mdierekezi, ndipo mungathe kuona kuti ndinu amene mukudzetsa chipsyinjo….Saturday kuti ndi Sabata la chipembedzo limandinyansa. Ndikudana nalo chifukwa Khristu akudana nalo!

"Inu mumadzitenga kuti ndinu mpingo wotsala?...ngati mukukhulupirira chomwecho, ndinu ozungulira mitu ndi odzitamandira. Chimenecho sichiphunzitso cha chi-Adventist!

"… monga mukuganiza kuti ponyoza kuti Saturday si Sabata, ndikunyoza chiri chonse chiri m'malamulo?...pakutero mukuganiza kuti ndine moyo wotaika ndi wachikunja?

"Alemekezeke Mulungu kuti atsogoleri a Chi-Senventh-day Adventist sakukhulupirira monga inu mukuchitira, ndipo iwo akuti, Ife taomboledwa ndikukhala amodzi mwa Khristu.

"Iwo amakhulupirira kuti ndinenso wobadwa mwatsopano. Ndine wopulumutsidwa ndiponso woyenera kulandira moyo wosatha. Akudziwa iwo kuti ndine wachi-Calvinist ndikuti ndapulumutsidwa kwa muyaya osati wotaika.

"(H) Ndinali ndi m'modzi wa amuna omwe anali patsogolo pokhazikitsa mgwirizano uwu m'Washington, D.C. m'November wapitayu yemwe anafotokozanso monga mukunenseramu. – (B) Munthu wake ndani?

"(H) …Mosabisa, ndi a Froom. Iwo anandiuza kuti anali ndi amuna inu kumsonkhano komwe munalonjeza kuti mukabvomereza kuti tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi la Sabata….

"(B) Ife timamva kuti tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi la Sabata….

"Panopa ndikulalikira motsutsana ndi za Sabata'lo.

"(H) …dziwani kuti atsogoleri athu amabvomereza zinthu zina kwa inu natiuzanso ife zosiyana.

"(B) Zoona, mungathe kulankhula izi m'mau ambirimbiri.

"(H) Paja munati muli ndi zolembera panopa zokuchitirani umboni pa chiri chonse chomwe mumachilemba m'magazini ya Eternity. Si nthawi yabwino ino yoti mungandionetseko zimenezo?

"(B) Zoona, koma-a-a-

"(H) Atsogoleri athu akukanitsitsa za izi. Tiyeni pano tikambirane zoona za chiphunzitso ichi.

"(B) Pakhala pali ma – Seventh-day Adventist amene akumaphunzitsa kuti Khristu anabadwa m'thupi la uchimo…Pano atsogoleri anu abwera poyera kukanitsitsa za chiphunzitsochi.

"(H) Atsogoleri athu'wo anali kumbali iti, yakuti Khristu anatenga thupi limene Adamu anali nalo asanachimwe, kapena ai?

"(B) …iwo akubvomereza kuti Iye anali Mulungu-munthu. Adamu analengedwa monga munthu wokhala ndi ufooko woti nkuchimwa. Koma Yesu Khristu anali Mulungu-munthu, wosati nkuchimwa.

"(H) Zalembedwa kuchokera ku nyumba zosindikiza mabuku za chi-Evanjeliko.Tikunenedwa kuti ife taima pakhomo la Bungwe la Umodzi wa Chi-Evanjeliko kugogoda kuti atitsegulire tilowemo.

"(B) …ndikukhulupirira, wina analankhulapodi za ichi, kuti a Seventh-day tsopano ali ndi mwai wakulowamo monga anachitira a Seventhday Baptist, ine kunalibe kumsonkhano umenewo …a Froom ndi anzao anali nao akuti a Walter Martin akudziwa zambiri za chi-Seventh-day Adventist kuposa wina ali yense wamaphunziro apamwamba aukachenjede [professor] m'Takoma Park, Washington.

"(B) Mkaziyu [Ellen White] amasowa chophunzitsa.

"(H) Mukukhulupirira kuti a Froom ndi a Anderson amagwirizana nanu pamenepo?

"(B) Ndikuzindikira kuti amuna amenewa ndi a nzeru zotha kuzindikira kuti mkaziyu sanali mngelo koma munthu woti nkuchimwa, ndipo ichi yekha anachilankhulanso.

"(H) Iwo anatsimikiza kuti zomwe walemba ndi zolakwika?

"(B) Inde akutsimikiza. Ali yense wa amuna amenewa anandiuza ine za ichi. Aliyense wa amuna'wa… ngati inu mungakhulupire monga anachitira atsogoleri anu oyambawo, chi-Seventh-day Adventist chidzabwereranso m'mbuyo ndi kukhala ngati chi-Mormon.

"Mkaziyu anali mai wabwino yemwe anadalitsidwa koma kwambiri kwake wolakwitsa zinthu.

"(H) Inu simukuganiza kuti atsogoleri a Froom ndi anzao akukhulupirira monga ndikuchitira ine? Kuti mai'yu anali mneneri woona?

"(B) Sakukhulupirira choncho amenewo.

Awa anali mapeto a zina za zokambirana pa lamya pakati pa a Al Hudson ndi a Barnhouse yemwe anamwalira patangotha zaka ziwiri kuchokera pomwe zinachitika. Koma a Hudson anachotsedwa mu mpingo chifukwa cholemba motsutsana ndi misonkhano ya a Martin-Barnhouse ndi atsogoleri athu.

## ZOCHITIKA KUCHOKERA 1960 MPAKA NTHAWI INO (1960-2008).

Bukhu la a Martin, TASDA Linasindikizidwa (February 1960) – A Martin anawatsimikizira a Anderson ndi a Froom kuti bukhu lao lidzaturuka nthawi imodzi ndi Mafunso pa Chiphunzitso ngakhale sizinatheke ndipo linaturuka pambuyo pa zaka ziwiri, m'February 1960, pomwe Choonadi za chi-Seventh-day Adventist [The Truth About Seventh-day Adventism (TASDA)] linasindikizidwa.

"A T.E. Unruh…anaulura kuti a Martin anapatsidwa zolembera zoyambirira [Manuscripts] za limodzi la Mafunso pa Chiphunzitso [QD] bukhu'lo lisanasindikizidwe; ndipo, iwonso analora atsogoleri athu kuwerenga zolembera zoyambirira za TASDA lisanasindikizidwenso. Awa ndi mau a koyambirira kwa bukhu la a Martin omwe analemba a Barnhouse:

"Zimveke bwino kuti tagwirizana chinthu chimodzi: kuti okhulupirira a chi-Seventh-day Adventist omwe akutsatira Ambuye mogwirizana ndi ziphunzitso monga azisinthira atsogoleri ao ndi okhawo atengedwe kukhala ziwalo zobvomerezeka za thupi la Khristu.

Pa tsamba 15 la bukhu la a Martin panalembedwa mau ndi a Harry W. Lowe,

Mkhalapampando ku Bungwe la Maphunziro a Bukhu Lopatulika ndi Gulu la Zofufuzafufuza la [Bible Study and Research Group] la General Conference ya a Seventh-day Adventist. A Lowe anayamikira kwambiri kubvomereza kwa a Martin za zikhulupiriro zomwe, a Froom ndi a Anderson analorera kuzisintha.

"Zolembera zake [Martin] pa zikhulupiriro zathu komanso kumasulira kwa maulosi… ndi zokhoza kwambiri…Mlembi'yu alandire kuyamikira kwathu ndi ulemu chifukwa chakuyesetsa kwake koona mtima polemba molondora bwino za zikhulupiriro zathu'zo."

Kumayambiriro kwa 1960. A F.D. Nichol analemba mau awa kwa a Figuhr: "Okhulupirira omwe si achi-Adventist adzawatanthauzira mau a Lowe'wa ngati kuti akulibvomereza bukhu'li.

A Martin anakhumudwa pamene malo athu ogulitsira mabuku anakana kuikamo bukhu lao, Choonadi za Chi-Seventh-day Adventist [TASDA].

Ndi liti pomwe bukhu la Choonadi za chi-Sevenbth-day Adventist linasindikizidwa koyamba? Pamene anthu ena akunenetsa kuti linasindikizidwa koyamba m'1960, a Froom akuti linasindikizidwa koyamba m'1957: "Bukhu lomwe ndiri nalo lalembedwa ndi kufalitsidwanso 1960." Kukanakhala kuti bukhu'li linayamba lasindikizidwa m'1957, zikanalembedwa pa tsamba lofotokoza za kusindikizidwa kwa mabuku. Magazini ya Ministry inayamba kufalitsa za kusindikizidwa kwa TASDA m'April 1960. Mosabisa mau, ichi ndi chitsimikizo chakuti a Frooom anali ndi chizolowezi chonena bodza. Anachita chonchonso ndi zolembera za Mzimu Wachinenero, chinthu chomwe chadzetsa chisoni chachikuru ku mpingo wathu. Iwo anali ndi luso longokhotetsa pang'ono choonadi, kuchipanga kukhala bodza.

**Msonkhano ndi a Barnhouse (kumapeto kwa 1959)** – M'February 1983, a Kem Pihl, M.D., a dotolo a chi-Seventh-day Adventist omwe anagwirapo ntchito yao ku chigawo chakumwera cha California, anandifotokozera ine kuti iwo ndi mkazi wao anakhalapo pa msonkhano wina wa a Barnhouse ku dziko la Amerika wa Kumwera, miyezi khumi ndi iwiri a Barnhouse asanamwalire. M'1959'mo n'kuti a Barnhouse ali ndi udani waukuru pa ma-Seventh-day Adventist, ziphunzitso zao kudzanso zolinga zao. Amaipidwa kwambiri ndi ma-Adventist. Kunali kumapeto kwa chaka chimenechi kuti iwo analankhula kwa ogwira ntchito ya Ambuye ku Amerika wa Kumwera.

A Dotolo a Pihl akufotokoza: "Kumapeto kwa 1959, mkazi wanga ndi ine tinali kugwira ntchito ku Peru monga antchito ya za chipatala a chi-Seventh-day Adventist.

"A Dr. Barnhouse anafika ku Lima. Poyambirira anaoneka achikondi kwambiri. M'modzi wa ogwira ntchito ya Ambuye anaima ndi kufunsa funso lopepuka kwambiri. Koma poyankha, a Barnhouse analankhula kwa kanthawi, mwadzidzidzi nkhope yao inafiira nayamba kulankhula ndi mau okwiya Kenaka anaomba m'manja napinda zala kupanga nkhonya ndi dzanja lao limodzi, ndikukhala ngati akumenya chinthu mwamphamvu, napfuula, 'M'dzina la Yesu Khristu, ndikutemberera Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri limenelo!'

M'mau onyoza omwe analankhula kuyambira pamenepo, zinadziwika kuti ananyansidwa nafe monga anthu. Pamene analankhula mau akuti 'Ndikulitemberera Sabata' mkazi wanga ananditembenukira ndikunena, 'Munthu uyu afa posachedwapa!' Pambuyo pake ndinadziulura kuti ndinali wogwira ntchito za chipatala wa chi-Adventist, ndipo poyankhanso, nkhope yao inafiiranso nandilankhula mokalipa, 'Ndikapitanso ku States, ndikaonana ndi atsogoleri a mpingo wanu m'Washington, D.C. ndi kuwauza za kubwereranso kwanu ku zikhulupiriro zanu zakale kumene inu ma-Adventist mukukuchita! Ndipo anabwerezanso kukulankhula kwao konyoza. Anali wokwiya kwambiri makamaka akamandiyang'ana ine monga wogwira ntchito wa chi-Adventist yemwenso ndinakhala patsogolo pao.

"Chisoni chachikuru chinandigwira chifukwa cha machitidwe ao oonetsa kuti anali ndi ulamuliro waukuru pa atsogoleri athu ku Takoma Park.

"Potsirizira ali chikwiyire kwambiri chomwecho, a Dr. Barnhouse analowa m'galimoto, ndikumenyetsa chitseko, ndi kumuuza woyendetsa kuti anyamuke."

"Zikuoneka kuti a Froom ndi a Anderson anawatsimikizira a Barnhouse kuti achotsa ogwira ntchito onse ku maiko achilendo komwe anatumizidwa!

**Imfa ya a Donald Grey Barnhouse (November 1960)** – A Donald Barnhouse anamwalira pa November 5, 1960, pafupifupi chaka chimodzi pambuyo pa zomwe zinachitika ku Peru, ali pamsinkhu wa zaka 70. Imfa yao inachitika pambuyo pa zaka zisanu zokha kuyambira pomwe inayamba kuchitika misonkhano ndi ma-Evanjeliko. Anakanthidwa m'September ndi nthenda yomwe inabvuta kuiturukira, ngakhale kumapeto kwake akatswiri a zachipatala anaipeza kuti inali zotupatupa zosati nkuchiritsika za m'bongo. Kanthawi kochepa kuchokera pamene anamwalira a Barnhouse, a Walter Martin anayambitsa bungwe lao la kafukufuku wa "chomwe chimapangitsa anthu kukakamira pa zikhulupiriro zosiyana ndi anzao ['cult research']."

**Imfa ya a William H. Brandson (1961)** – A William Henry Brandson (1887-1961) anali mmodzi wa amuna amene kwa zaka zambiri anatsogolera pakutchinjiriza chiphunzitso chachikalekale cha chi-Adventist. Ndipo ndi zodziwika bwino kuti ngati akanakhalabe Presidenti, misonkhano ndi ma-Evanjeliko ( inayambayo m'1955) sikanachitika.

**Imfa ya a M. L. Andreasen (1962)** – Zolembera zotsatirazi zikupatsani inu chithunzithunzi cha chisoni chachikuru chomwe munthu wa Mulungu, a M.L. Andreasen anachimva, ndi kuwapangitsa kuti amwalire:

"Tsiku limene'lo [nyengo ya masika 1956], atangowerenga zolembera za Bombalaphulika zomwe a Barnhouse anangozisindikizanso kumene m'magazini ya Eternity, a M.L. Andreasen anailowa ntchito yakutsutsa mosatopa yomwe inachepetsa nthawi ya moyo wao..

"Chidwi cha Andreasen chinakopeka ndi mau: 'Monenetsa, zatsimikizika kuti ma-Adventist akukanitsitsa kotheratu zina za ziphunzitso zomwe nthawi yonse yambuyomu zimatchedwa zao.'

Kupitiriza apo a M.L. anawerenganso: 'Chiphunzitso ichinso chakanidwa kotheratu.' Chiphunzitso chiti? Chikanakhalanso china chiti kuposa cha Kachisi wakumwamba ndi nsembe yotetezera – chomwe kwa zaka zochuruka panakhazikikapo chikhulupiriro chathu.

A M.L. anawerenganso: 'Iwo [ma-Adventist] sakukhulupiriranso zina zomwe atsogoleri ao oyambirira anaziphunzitsa, kudzanso chakuti nsembe yakutetezera ya Yesu sinathere pa Gologotha.'

"Mosakhalitsa magazini ya Ministry inafotokoza kuti mayankho akuya pa nkhani'yi adzafalitsidwa m'bukhu lomwe lilembedwe: 'Amuna ena 250 m'Amerika ndi ku maiko ena alandira kale zolembera zoyambirira [MSS] za bukhu lomwe lilembedwe'lo. Ndipo ambiri alibvomereza.'"

A Virginia Steinweg, alemba m'magazine ya Popanda Mantha Kapena Kokondera [Without Fear or Favour:] Amuna 250 omwe analandira zolembera za bukhu'li zisanasindikizidwe ndi ndani?

"Ichi anabvutika nacho maganizo pozindikira kuti sikuchuruka m'chiwerengero momwe mumakhala chidziwitso chokhoza. Palibe udindo mu mpingo womwe unampanga munthu katswiri pa za chipembedzo. Ndiponso kuti nkosatheka woweruza mumpingo kukhala mbusa kapena mbusa kukhala woweruza.

"Chinthu chimodzi a M.L. anachidandaula kwambiri chinali chakuti: anthu amene akanatha kutsutsa zolakwika mu zokambirana za ziphunzitso za nsembe yakutetezera ndi umunthu wa thupi la uchimo za Khristu sanapatsidwe mwai wakukhala m'misonkhano imachitikayo."

Ataona kuti makalata otsutsa sanasamalidwe, Andreasen anayamba kuchenjeza anthu athu pakulemba ndi kutumiza pamtengatenga. Kenaka ntchito yake inatsekerezedwa. Mabuku ake anachotsedwa m'malo athu ogulitsira mabuku m'November 1960; ndipo pa April 6, 1961, makalata ake a za ubusa analandidwa.

"A Steinweg akupitiriza: Thanzi la a M.L. silinathe kulimba ku chisoni chimene anali nacho, maka kuti amakhala mausiku aatali osagona. Sanaloredwenso kulalikira ulaliki



ndi umodzi womwe la Sabata.. Usiku wao wotsiriza iwo sanagone koma kupemphera ndi kulira m'nyumba mwao. Mkazi wao anatumiza uthenga kwa a Prezidenti a General Conference [R.R. Figuhr], omwe pa nthawiyo anali pafupi, kuti a M.L. anafunitsitsa ataonana nao.

"A M.L. anafotokoza momveka bwino za dandaulo lao pakayendetsedwe ka nkhani yosintha ziphunzitso'yo, ngakhale anasiyana nao maganizo pa njira zomwe anazitsatira, iye anafunitsitsa kusiyana ndi abale akewo mwa mtendere. Munadzala misozi ya chimwemwe m'maso mwao pamene analawirana nao alendo ao'wo. "Pano ndingathe kufa mumtendere," anamuuza mkazi wao.

Tiri ndi chiyembekezo chodzakomana nayenso munthu wa umulunguyu, a M.L. Andreasen kumwamba; pantchito yaikuru anaichitayo yakuchenjeza anthu a Mulungu za choipa chomwe chinali kuchitika. Pa March 1, 1962, komiti GC inabwezera makala a ubusa a Andreasen. Chikanakhala chinthu chokondweretsa ngati pakutero komiti'yo, ikanaletsanso kufalitsidwa kwa bukhu la Mafunso pa Chiphunzitso. Monga zakhala zikuchitikira mu mbiri ya dziko, ali yense amene anachenjeza anthu za choipa chinali nkudza amatchedwa wosokoneza ndi woyambitsa mabvuto.

**A R.R. Figuhr Alowetsa a B.B. Beach mu Komiti ya Bungwe La Mipingo ya Dziko lonse [WCC] (1965)** – A Figuhr anakonzetsera kuti a B.B. Beach akhale chiwalo cha bungwe la mgwirizano wa zipembedzo, kwa nthawi

yoyamba mu mbiri ya mpingo wathu.

A Figuhr Apumula pa Udindo wa Uprezidenti (1965) – Pambuyo pakuononga kosati nkukonzanso, a Figuhr anapumula atakhala paudindo wa Prezidenti kwa nthawi ya zaka 12.

Bukhu la A Froom, Kusintha ndi Cholinga [Movement of Destiny] (1971) – Pambuyo pa zaka khumi bukhu la Mafunso pa Chiphunzitso litasindikizidwa, a L.E. Froom anasindikiza bukhu lao lofotokoza mabvuto a za chiphunzitso cha mau a Mulungu a 1888 ndi a m'ma 1950, lotchedwa Kusintha ndi Cholinga [Movement of Destiny]. Ndi zochititsa chidwi kuti sipakupezeka pena pali ponse pomwe a Schuyler English, Walter Martin, kapena a Donald Barnhouse abvomerezapo chiphunzitso chathu ndi chimodzi chomwe! Kulolera kuli konse kumachitidwa kuchokera kumbali yathu. Kuyambira pachiyambi mpaka chimaliziro, ma-Evanjeliko a Mpanduko ndiwo anapereka ziphunzitso za momwe chiyero chinayenera kuchitidwira. Kusintha ndi Cholinga, linalembedwa mozungulirazungulira ndi cholinga chofuna kutitsogolera momwe pang'ono ndi pang'ono tinayenera kusiyira zomwe amati ndi ziphunzitso zolakwika za atsogoleri athu oyambirira. Ndi zoona kuti a Froom ndi a Martin sanasinthe chiphunzitso chathu cha Kachisi wakumwamba. Chimene anachita chinali kukhazikitsa maziko olimba a ziphunzitso zolakwika zomwe pano zikulimbana ndi kuthetsa chiphunzitso chathu cha Kachisi'cho. A Martin ndi a Froom anapereka chipolopolo; chiphunzitso cholakwika chatsopano za mau a Mulungu mfuti yoomberera chipolopolocho; ndipo panopa kuombera kukuchitika. Okhulupirira ambiri agwa ndi kubvulala, osatinso nkuchira. Chiyero cha pa ziphunzitso, kumapeto kuno, sichikuwerengedwanso koma mgwirizano ndi mipingo yopandukira Mulungu ndiwo.

Molingana ndi a Froom, cholinga cha kusintha kwathu ndi chakuti tiyanjane ndi mipingo yakugwa. Ndipo kuti ichi chitheke bwino, tisiye kulalikira Danieli 7 ndi Chibvumbulutso 12, 13, ndi 14. Monga nkutheka ife kukhala mpingo wotsala titasiya kulalikira uthenga wa Chibvumbulutso 14:1 mpaka 12?

Kusintha mu Zoonjezera B (1972) – Kusagwirizana kwa a Martin ndi ziphunzitso za chitetezero ndi umunthu wathupi lauchimo la Khristu kunali kwakukuru. Ife tinazindikira kuti ngati titabvomereza kusintha kwa ziphunzitso ziwirizi, ndiye kuti tabvomereza kupondereza choonadi chofunika kwambiri cha kumvera ndi kusunga malamulo a Mulungu. Koma mosazindikira choopsya ichi, a Froom ndi a Anderson anagonjera. A Martin anaoneka a nzeru kuposa awiri'wo. Kenaka a Martin ndi a Barnhouse anatembenuka nafunsa za maganizo athu za ziphunzitso zoyambirira za chi-Adventist maka ziwiri'zi.

M'1971, a Froom analiyamikira "gulu" lao pa zokambirana zomwe linazichita pa ziphunzitso zimenezi: "Kwa zaka zambiri, kufufuza kotheratu m'zolembera zonse za Mzimu Wachinenero kunachitika, kokhazikika pa mafunso ofunikira ..

Zonse'zo zinalembedwa m'Mafunso pa Chiphunzitso, monga ziri m'zolembera Zoonjezera A [umulungu wa Khristu], B [Umunthu wa thupi la Khristu], ndiponso C [Chitetezero]. Umu ndimo inatsirizikira ntchito yakutanthauzira,… Wogwira ntchito ndi wophunzira za ubusa ali yense ayenera kumakhala ndi zolembera zoonjezera izi monga zomthandizira."

Kumbukirani kuti a R.A. Anderson mwachinsinsi anasintha Zoonjezera B kumapeto kwa Bukhu 7A Lomasulira Mau a Mulungu [Seventh-Day Adventist Bible Commentary, Vol. 7A]. Ndipo iye anachichita ichi mwa yekha mosayamba wadziwitsa ngakhale akonzi okonza zolakwika m'mabuku!

Pambuyo pa zaka khumi izi zitachitika, m'1970, kufufuza kosamalitsa kutachitika m'maofesi a akonzi a mabuku ndipo anaturukira zomasulira Mau a Mzimu Wachinenero zolakwikazi.

A Herbert Douglass akufotokoza: "Komalizira kweni kweni ndinapeza mpata wowerenga mofatsa maumboni a m'QD… tonse tinayang'anizana kuona kumasulira kosaganizira chomwe chinali cholinga cha zolembera'zo.

M'1972, A bungwe la Kafukufuku wa Bukhu Lopatulika [Biblical Research Institute] anayesera kukonza zolakwika kuyambira m'Zoonjezera B, m'QD ndiponso Bible Commentary 7A.

A Froom Anaturukira Choonadi Asanafe (1974) - Ndi zosangalatsa kuti zomasulidwa Zoonjezera B zinasindikizidwa zaka ziwiri a Froom eni ake asanafe. Zikuoneka kuti anatsutsika.

Mkazi wa a "Jim," yemwe anali wokonzetsera zolembera za a Froom akufotokoza, "Pamene a Froom anangotsala pang'ono kumwalira, anaitanitsa a Jim. Chimene a Jim anachiona pa nkhope ya a Froom anali mantha chifukwa cha zolakwika anazichita'zo m'zaka za m'mbuyomu, koma panthawi'yi anali akuyang'anizana ndi mapeto a moyo wao… Ndithudi, a Froom anakumbukira choipa anauchitira mpingo wotsala wa Mulungu."

Kuletsa Kusindikizanso Mafunso pa Chiphunzitso ndi Kusintha ndi Cholinga (1975) - Patapita chaka chimodzi a Froom atamwalira, mabuku ao awiri analetsedwa kuti asasindikizidwenso.

A Douglass akufotokoza: "Nthawi iri yonse bukhu'li [QD] linakhala likufufuzidwa, linakhala likuumitsiraumitsira mtima [atsogoleri a GC], kuti asalilore kusindikizidwanso.

"Kuonjezera apo, chifukwa cha zolakwika zambiri zomwe zinalinso zosokoneza, The Movement of Destiny nalo linaletsedwanso."

Mgwirizano wa ku Dallas (1980) – Msonkhano wa General Conference wa ku Dallas, Texas, (1980) unagwirizana zolemba bukhu lomwe likomere onse otsutsa ndi obvomereza zikhulupiriro ndi ziphunzitso zatsopano mu mpingo. Ndipo Bukhu la Zikhulupiriro za a Seventh-day Adventist [Beliefs of Seventh-day Adventists (27 Fundamental Beliefs)] linabvomerezedwa ndi onse ndi kulembedwa.

Izi ndi ziphunzitso ziwiri zosokonezanso m' bukhu la 1980'li: "Iye anakhala munthu ndithu, Yesu wotchedwayo Khristu. Anaikidwa m'mimba ndi Mzimu Woyera ndikubadwa ndi Mariya namwaliyo. Anakhala moyo ndi kupezana ndi mayesero monga munthu, koma mwaungwiro wake anakhalabe m'chilungamo ndi chikondi cha Mulungu." [Mau onena za thupi la uchimo la Khristu sakutchulidwa.]

"Muli Kachisi m'mwamba, chihema choona chimene Ambuye anachimanga si munthu ai. M'Kachisi ameneyu Khristu akutetezera m'malo mwathu, ndikupulumutsa okhulupirira onse mwa mwazi wake wakutsuka machimo umene unakhetsedwa kamodzi pa mtanda chifukwa cha machimo a anthu onse."

A Julius Nam akufotokoza: "Kuyambira pamene bungwe la Review ndi Herald Publishing Association linasiya kusindikiza bukhu [QD] mu 1975, bungwe la General Conference silinakanepo kapena kulitchinjiriza bukhu'lo….Zolembera zimene Bungwe la General Conference linazibvomereza kukhala maziko a chikhulupiriro cha mpingo[Fundamental beliefs] ku msonkhano wa 1980 zinali zongokweza Mafunso pa Chiphunzitso lomwe likukweza mtanda ndikupondereza utumiki wa Khristu uja unayamba 1844 m'Kachisi wakumwamba ndipo uli kupitiriza kwa nsembe yakutetezera machimo yomwe inayambira pamtanda." – Ndipo kukonzanso ziphunzitso kunachitika m'2005 kumsonkhano wa GC ku St. Louis kunali konyansitsitsa kwa misonkhano yonse! Zambiri pa mpfundoyi pambuyo.

Kumwalira kwa Ruben R. Figuhr (1983) – Ndizosabisika kuti a Figuhr ndiwo kawirikawiri anali mkhalapampando wa misonkhano ya a Froom, a Anderson ndi a Martin.

Pakutengako mbali mosalekeza, iwo anakhuzidwa ndi zolakwika zonse zimene zinachitika pofuna kungokondweretsa a Martin. Patangokhala chaka chimodzi kuti apume ntchito, a Figuhr anakonzetsera kuti a Bert Beverly Beach akaimire mpingo kwa nthawi yoyamba mu mbiri ya mpingo wathu ku komiti ya Bungwe la Mgwirizano wa Mipingo Yonse ya Dziko Lapansi [WCC].

Chotsatira chakulowa mu mgwirizano wa 1965, chinali chakuti mpingo wathu unatha mantha ndi kulowerera mkati mwa migwirizano ya Umodzi wa Zipembedzo, ndikunka ukusendera chifupifupi kwambiri kwa mipingo ina.

Msonkhano wa a Martin ku Napa (1983) – Cholinga cha msonkhano uwu chinali chakuti a Martin aliopsyeze bungwe la General Conference kuti ngati silisindikizanso [QD], iye alemba bukhu lonyanzitsa mpingo wathu.

A Martin anati (osati Bukhu Lopatulika koma) bukhu la Zikhulupiriro Za Chikhristu [Creeds of Christendom], lokhala ndi "ziphunzitso" zonse za mipingo yoona ya chikhristu. Iye anafotokoza kuti sanautche mpingo wa Katolika gulu la anthu wochita zachipembedzo mosinjirira [cult] chifukwa uli nao makhazikitsidwe akale a chifupikitso cha chikhulupiriro chake [creeds].

Nanga kagulu kochita chipembedzo mosinjirira kamakhala kotani? Ndi timagulu tomwe timaswa malamulo a Mulungu ndi kuphunzitsa kuti tidzapulumuka tiri chikhalire mu uchimo. Nanga wotsutsana ndi Khristu ndi ndani? Ndi munthu ali yense wokana kuti Khristu sanali munthu ndipo sanadzitengere pa Iye mwini thupi lathu lauchimo'li!

Kotale ndi Bukhu la a Gulley (1983) - Kotale woyamba wa miyezi itatu yoyambirira ya 1983 anali Adventist Kotale wa Akuruakuru[Adventist SeniorQuarterly] yemwe anali ndi zolakwika za m'QD. Uyu pamodzi ndi bukhu limene amayendera nalo limodzi, Khristu Nkhoswe Yathu [Christ Our Substitute], anali mabuku oyambiria kupereka ziphunzitso zosokonekera zatsopano. Zinthu zinapitirira kuipa kwambiri, pamene a Gulley, anasankhidwa kulemba zolembera zoyambirira za bukhu la chiphunzitso lotchedwa Zikhulupiriro za A Seventh-day Adventist [Seventh-day Adventist Believe (SDAB - 27 Beliefs)] lomwe linalowa m'malo mwa QD! Ndi chifukwa chiyani atsogoleri anasankha munthu amene analemba kotale ndi bukhu zomwe zinanyoza zikhulupiriro zathu zofunikira kwambiri? Litangosindikizidwa SDAB m'1988 zonse zimene amadandaula a Walter Martin ndi mpingo wao zinasiyikiratu.

A Martin alembanso Ufumu wa Timagulu ta Tizipembedzo Tosinjirira [Kingdom of Cults] (1985) – Bukhu la Ufumu wa Timagulu ta Tizipembedzo Tosinjirira lakhala chiri cholakalaka cha Martin kuti alilembe.

A Martin analemba: "Pa February 18, 1983, ndinalembera ku General Conference ya Seventh-day Adventist (Washington D.C.), kuwafunsa kuti abvomereze kapena kukana poyera kuti ndiwo analemba bukhu la Mafunso pa Chiphunzitso."

Taganizirani za tsiku'lo: February 18, 1983. Kalata yakeyi anailembera ku General Conference patangotsala masiku anai kuti akapereke phunziro ku Napa. Iye amafuna kuwaika a General Conference'wo pampanipani kudzera m'machenjezo ake awiri otsatana. Ndi m'phunziro lake la ku Napa,

kuti iye anakakamiza General Conference kuti isindikizenso Mafunso pa chiphunzitso. Ichi anachichita ndi cholinga chofuna kuwaonetsera atsogoleri athu (komanso a mipingo ina) kuti iye anali ndi ulamulironso pa ziphunzitso zathu.

A Martin akupitiriza kufotokoza kuti analandira yankho (pa April 29) kuchokera kwa a W. Richard Lesher omwe anati: "Muyambe mwafufuza choyamba ngati a Seventh-day Adventist akugwirizanabe ndi mayankho omwe anaperekedwa ku mafunso anu m'Mafunso pa Chiphunzitso monga anachitira m'1957. Yankho ndi lakuti inde…"Gulu lalikuru la a Seventh-day Adventist akugwirizana ndi ziphunzitso za m'Mafunso pa Chiphunzitso."

Ichi chinaika General conference pobvuta. Monga kudzatheka – kuti kumapeto iturukemo – ndikumasuka bwinobwino kuchoka m'manja mwa a Martin, kapena inalolera kugonjera monga zinachitikira m'zaka za m'ma 1950?

Chifukwa cha ichi m'malo mosindikizanso QD, General Conference inasindikiza la ziphunzitso lina [SDAB] kulowa m'malo mwa QD'lo.

Kukambirana ndi a Ankerberg (January 1985) – M'January 1985, a William Johnsson ndi Walter Martin anakwera ndege kupita ku Chattanooga kukajambulitsa ma-video ndiponso zokambirana za pa wailesi ya kanema. M'malo mokhala monga munthu wopanda mbali (chomwedi chinali choti akachite), a Ankerberg anakhala kumbali ya a Martin nasinthana pakufunsa mafunso olimba ndi amsangamsanga omwe ngakhale pakanakhala ma-Adventist ophunzira ndi wodziwa ziphunzitso zathu bwino kwambiri sakanatha kuyankha.

Ofunsa mafunso'wa makamaka anakhazikika pa zinthu zitatu:

(1) Ngati inu ma-Adventist mumabvomereza zolembera za mkazi [E.G. White] monga zokutsogolerani mu mpingo wanu, ndiye kuti ndinu kachipembedzo kochita za chipembedzo mosinjirira kuposera muyeso [cult].

(2) Ngati inu ma-Adventist mukubvomereza ziphunzitso izi [Kachisi wakumwamba, chiweruzo chakufufuza mu mtima ndiponso cha chitetezero cha m'Kachisi wakumwamba] zomwe mulibe m'bukhu lanu la ziphunzitso la Mafunso pa Chiphunzitso, ndiye kuti ndinu opandukira banja lonse la mipingo ya Mpanduko.

(3) Ngati inu ma-Adventist mumabvomereza kuti palidi chitsimikizo chakuti mkhristu ali yense ayenera atengeko mbali ndi kugwira ntchito ya chipulumutso chake, ndiye kuti ndinu achilamulo monga anali Afarisi osati akhristu.

Ngati mdani angathe kutisokoneza pa ziphunzitso zitatu izi za chikhulupiriro chathu, ndiye kuti ndi chipambano chonse angathe kuononga maziko a ziphunzitso zonse zomwe timadziwika nazo!

Tikafuna kudzitcha tokha kuti tikulalikira chi-Adventist lero lino, a Johnsson akuti chikhulupiriro chathu chikhazikike kwatunthu pa ziphunzitso zomwe zinabvomerezeka ku Dallas [zikhulupiriro (27 Beliefs)]! Izitu zikutipanga ife kukhala mpingo wokhulupirira m'ziphunzitso za umunthu m'malo mozikika m'Mau a Mulungu.

A Luther anachifotokoza chikhulupiriro chao m'mau akuti: Ndiyenera ine kuweruzidwa "ndi chinthu chimodzi chokha, iwo agwiritse ntchito Mau a Mulungu kukhala muyeso wao. Anthu alibe udindo wina woti achite, koma kumvera Mau a Mulungu." "Munditsimikizire kuchokera kuzolembera za aneneri ndi atumwi ngati ndalakwa." "Ndiri ndi mantha akuru kuti masukulu a za ukachenjede adzakhala zipata za chitaiko, pophapokhapo ngati atalimbika kukhazikika m'Malembo Oyera..Sindikulimbikitsa munthu ali yense kutumiza mwana wake kumene Mau a Mulungu sakulamulira. Bungwe lina liri lonse kumene anthu ake sali m'Mau a Mulungu, limakhala losokonekera."

Imfa ya a R.A. Anderson (1985) – Atsogoleri a Anderson ndi mphamvu zao zonse anawatchinjiriza a Martin ndikuti anali "bwenzi loposa" la mpingo wa Seventh-day Adventist. Anali atsogoleri a Anderson omwe analankhula mwatchutchutchu kuti cholinga cheni cheni cha Mafunso pa Chiphunzitso chinali kufuna kuzikonzanso zikhulupiriro za mpingo wathu.

M'1956, a Anderson analemba makalata awiri kwa a R.A.Greive, prezidenti wa bungwe Lalikuru la mpingo ku Australia [Australian Conference yemwe pambuyo anachoka mu mpingo wa Adventist.] A Greive amaphunzitsa chiphunzitso chakuyeretsedwa pa nthawi yomweyo, kutanthauza kuti munthu akangomlandira Khristu nthawi yomweyo angathe kulowa kumwamba, ngakhale asamvere, kuchita ndi kusunga malamulo a Mulungu.

M'makalatamo, a Anderson anagwirizana ndi a Greive kuti Khristu sanakhala m'thupi lathu la uchimo'li, ndipo a Anderson awatsimikizira a Greive kuti posachedwa ziphunzitso zao'zo zibvomerezedwa ndi anthu ambiri amene a Anderson'wo amachita nao misonkhano ndi ma-Evanjeliko. Koma panthawiyo, a Anderson anachenjeza a Greive kuti asauze munthu wina ali yense mpaka mtsogolo.

Herb Douglass akufotokoza: "Kwa zaka zambiri pambuyo pakupuma ntchito kwa a Dr. Anderson nakhala iwo m'nyumba yao yomwe inali chipinda chimodzi m'Loma linda, anakhala akundiyimbira mafoni kawirikawiri. Mafunso amene amakonda kufunsa anali, 'A Herb, chikuchitika ndi chiyani ndi mpingo wathu?' Zikuoneka kuti awiri'wa [a L.e. Froom ndi a R.A. Anderson] amadzimvera chisoni pa zimene anauchitira mpingo m'zaka za ma'1950."

Mabuku a a Ralph Larson (1986) – A Ralph Larson anali mtchinjirizi wamphamvu wa chiphunzitso chachikalekale cha chi-Adventist. M'bukhu lao "Mau Anasandulika Thupi"[The Word Was Made flesh], akufotokoza mwatsatanetsatane za (Zolembera za Mau a Mzimu Wachinenero ndi za alembi ena) omwe akutsimikizitsa kuti Khristu anatenga thupi lathu la uchimo'li. M'kufufuza kwao a Larson akuti sanapeze mlembi wa chi-Adventist ndi m'modzi yemwe patsogolo pa 1952 yemwe analembapo motsutsana ndi chiphunzitso chakuti Khristu anatenga thupi lathu la umunthu, la uchimo'li! Ndiponso kuti kwa nthawi pafupifupi zaka makumi asanu ndi limodzi, Mlongo White sanasinthepo za chikhulupiriro chake chakuti Khristu anatenga thupi lathu la umunthu , la uchimo'li!

M'bukhu lao "Lalikira za Mphamvu Yake [Tell of His Power], la 1988, a Larson analembamo maumboni okwanira 1,200 kuchokera m'zolembera zosiyanasiyana kuyambira za m' Amerika wa Kumpoto, Great Britain, South Africa ndi Australasia. Mwa maumboni onsewo pafupifupi 400 anatengedwa m'zolembera za a Ellen White.

Zolembera Zoopseza za a Sample (1988) – M'zolembera zokwanira masamba 15 zopezeka m'Kufufuzafufuza za Chikhristu za Tsiku ndi Tsiku [Christian Research journal], a Sample anawafotokoza "ma-Evanjeliko Adventist"(dzina limene anawapatsa ena a ife amene analorera ziphunzitso zatsopano) kuti akuzunzidwa ndi kuthamangitsidwa mu mpingo wa Adventist. Patangopita nthawi pang'ono, bukhu lathu latsopano la ziphunzitso, Zikhulupiriro za a Seventh-day Adventist (SDAB) linaturuka kuchokera komwe limasindikizidwa; ndipo zolankhulalankhula zonse zotitchula maina achipongwe zinasiyika nthawi yomweyo. Ichi chinali chifukwa chakuti SDAB linali ndi ziphunzitso zolakwikanso monga momwe zinali mu lomwe linaliyambirira [QD].

Zomwe a Martin anazichita m'1983, anazichitanso m'1988 kudzera m'zolembera za a Sample. Mu nthawi ziwiri zonsezi, a Martin anafuna kuti ma-Evanjeliko pena pali ponse azindikire kuti ndi chifukwa cha kuopseza kwa a Martin'wo kuti ma-Adventist anapitiriza kugonjera zofuna zao.

Kusindikizidwa kwa bukhu la Zikhulupiriro za a Seventh-day Advemtist 1988 – Chifukwa cha kukangana kosatha za QD, bukhu'li linaletsedwa kuti lisasindikizidwenso. Koma m'1983, a Walter Martin anayamba kuwaopseza atsogoleri a mpingo wathu poyera.

Choncho, m'1988, bukhu lokhala ngati QD linafalitsidwa. Ili linatchedwa Zikhulupiriro za a Seventh-day Adventist (SDAB [27 Fundamental Beliefs]), ndipo linali ndi ziphunzitso zolakwika zambiri monga momwe linali bukhu loyamba'lo. Chifukwa cha ichi zolembera zoopseza ndi zotinyoza zomwe a Martin anazilemba sanazisindikize. Tinagonjera kuzofuna zao. Chonde zindikirani ndi kumvetsetsa kuti SDAB ndi bukhu lomwe linabvomerezedwa kufalitsidwa ndi mpingo wathu.

Kufalitsidwa kwa QD kunachedwa ndi nthawi yoposera chaka chimodzi, chifukwa chokanidwakanidwa ndi osindikiza mabuku a Review komanso ena a atsogoleri athu. Pamene SDAB linatsala pang'ono kuti lisindikizidwe, masamba oposera 75 anachotsedwa m'bukhu'lo! Chotsatira chake chinali kusakanikira kwa choonadi ndi mau ena olakwika omwenso anapezeka m'mabuku onse awiri. Choncho ichi chikuwapangitsa mabuku onse awiri'wa kukhala oopsa kwambiri. Palibe paliponse mu Kotale wa gawo lachitatu wa Maphunziro a Sabata Sukulu wa 1988 pomwe bukhu latsopano'li linalengezedwa kuti ndi lothandizira pakuphunzira Kotaleyo. Chinachititsa chinali chiyani?

Mau anatumizidwa ku nyumba yosindikizira mabuku kuti pafupifupi masamba 75 anachotsedwa m'bukhu la ziphunzitso latsopano'lo! Choncho kuchuruka kwa zolembedwa zomwe zinachotsedwa apa ndi apo kuchokera m'bukhu latsopano'li zinakwanira gawo limodzi la magawo asanu a zolembedwa zonse zinali m'menemo.



Monga momwe a Leroy Edwin Froom anali mlembi wa Mafunso pa Chiphunzitso, chomwechonso a Norman Gulley anali mlembi woyambitsa ndi wotsogolera wa Zikhulupirio za a Seventh-day Adventist.

Zaka zisanu ndi chimodzi zinapita m'mbuyo, a Gulley anali atalemba Kotale wonyansitsitsa wotchedwa, Kotale Wa Akuru wa 1983 ndi bukhu lothandizira pakumphunzitsa lotchedwa Khristu Nkhoswe Yathu [Christ Our Substitute]. Ichi

chinawaonetsera iwo kuti anali wauzimu wokondera mbali yosokoneza. – Koma chodabwitsa nkukhalanso chakuti a Gulley omwewo anasankhidwa kulemba bukhu la ziphunzitso za mpingo! Mutu wakuti Khristu Nkhoswe Yathu (COS) unali ndi tanthauzo lakuti Khristu ndi nkhoswe yathu m'zinthu zonse, kuphatikiza kutipatsa mphamvu yakumvera komwe Mulungu amakufuna kuti atipulumutse nako, ngakhale ife tisafune kumverako.

Mau a Bungwe la Zofufuzafufuza za m'Bukhu Lopatulika (1989) – Pambuyo pa kanthawi kochepa kuchokera pomwe a Ralph Larson anasindikiza maumboni ao ochuruka omwe anawasonkhanitsa okhuza nkhani ya ziphunzitso'yi, Bungwe la Zofufuzafufuza za Mau a Mulungu [Biblical Research Institute (BRI)] la GC linasindikiza bukhu ku Review lomwenso likukanitsitsa za kufunikira kwa ziphunzitso zathu za choonadi za chikakekale zomwe zinakanidwanso m'bukhu la Mafunso pa Ziphunzitso!

"Mpingo wa Dziko Lapansi Lonse'wu sukuona kuti ziphunzitso izi: [Chikhalidwe cha chiyero cha Khristu ndi cha kuipa kwa uchimo] ndi zofunika kwambiri pa chipulumutso ndiponso kuchipambano cha utumiki wa mpingo wotsala…'Ziphunzitso izi ziyenera kuikidwa pambali osati kuwalemeretsa anthu athu ngati kuti ndi zofunikira kweni-kweni.'"

A Walter Martin anagonjetsa pa nkhondo yao yotsiriza yakusokeretsa miyoyo ya ziwalo zambiri za mpingo wa Adventist. Patangotsala nthawi pangono kuti bukhu la BRI liturutsidwe, a Martin anamwalira.

Imfa ya A Walter Martin (March 1989) – Pa March 15, 1989, a Martin mwadzidzidzi anabwereranso kuyamba kuchitiranso mtopola ziphunzitso za chi-Adventist mu msonkhano womwe anachititsa m'Fresno,- California. M'kalankhulidwe kao ananyoza kwambiri Mau a Mzimu Wachinenero ndi udani waukuru womwe sanauonetsepo ndi kale lonse.

Pambuyo pa msonkhano umenewu anakonzanso wina; uwu unali woti ukachitikire pafupi ndi Loma Linda. A Martin anakonzekera ndi kulemba zonse zomwe anati akalankhule ndipo tsiku linalengezedwa: Lolemba, June 26, 1989. Kulankhula uku kunali koti akatsutsane molimbika kwambiri ndi chi-Adventist.

A Martin anadzuka m'mawa ku nyumba yao ku San Juan Casistrano, California, - mwadzidzidzi nthenda ya mtima inawagundikira. Ndipo pofika iwo kuchipatala anali atafa kale. N'zosaiwalika mu mbiri ya dziko kuti a Martin, osakhala a chi-Adventist anausintha mpingo wa Seventh-day Adventist kuposa munthu wina aliyense!

Mulungu akanatitchinjirizatu ife ku ziopsezo za a Walter Martin kuyambira m'ma 1955, ngati tikanakangamira kotheratu pa Bukhu Lopatulika/Mau a Mzimu Wachinenero monga maziko a ziphunzitso za chikhulupiriro chathu. Koma iye sanatero. M'zaka zakutsogolo kuno, kufikira m'1980, zotsatira za chonyansitsitsa chakupululutsachi zikuonekera. Pa tsiku la chiweruzo chotsiriza ndi pomwe nthano yonse idzadziwika bwino.

Chonde, okondedwa awerengi, werengani Bukhu Lopatulika ndi Mau a Mzimu Wachinenero tsiku ndi tsiku ndi kumvera chomwe Mau oyerawo akufuna; pomwepo mudzatchinjirizidwa.

Kufalitsidwa kwa QD Lokhala ndi Mau Omasulira (2003) – Sukulu ya Za Ukachenjede ya Andrews inalisindikizanso QD pambuyo pa zaka zoposa makumi awiri. Ili linali bukhu leni leni la QD lokhala ndi mau oonjezera ndi ndemanga za a George R. Knight zomwe zikupezeka m'bukhu lonse'lo.

Chiphunzitso cha a Knight mu ndemanga ndi mau omwe anaonjezera'wo ndi chakuti QD linangosintha chiphunzitso chokhuza umunthu wachikhalidwe cha Khristu…Koma maumboni ochuruka akuonetsa kuti ziphunzitso zambiri, osati chimodzi chokha, zinasinthidwa.

Lumbiro Latsopano la Ubatizo (July 8, 2005) – "Chiphunzitso" cha chi-28 chotchedwa "Kukula Mwa Khristu [Growing in Christ!"] sichinatchulepo chiri chonse zakufunikira kwa kumvera lamulo la Mulungu, kapena chiri chonse cha zomwe Mulungu akufuna!

Kuonjezera apo, lumbiro lina latsopano la Ubatizo, lomwe linakhazikitsidwa m'2005 (pa July 8), ndipo, ndiloipitsitsa la onse. Liri ndi ziganizo zitatu zokha! Izo zikungoti: (1) Landirani Khristu. (2) Khulupirirani Bukhu Lopatulika monga momwe linatanthauzidwira kumsonkhano wa ku Dallas. (3) Bwezerani zachikhumi ndi zopereka. – Izi ndi zokhazo munthu ayenera kuzichita ngati akufuna kukhala chiwalo cha mpingo wa Adventist komanso ndi chitsimikizo chodzalowa kumwamba!

Pa Msonkhano Wakukwaniritsa zaka 50 kwa Bukhu la QD (2007) - Pa October 24-27, 2007 unachitika msonkhano wa masiku anai ku Sukulu ya Za ubusa ya Sukulu ya Ukachenjede ya Andrews komwe kunaperekedwa maphunziro 24, ena ndi anthu obvomereza, ena ndi otsutsa, komanso enanso ndi aphunzitsi amene sanali a chi-Adventist koma a chi-Evanjeliko. Kuphunzitsako kunachitika mogwirizana ndiponso motsutsana ndi bukhu'lo [QD].

Aphunzitsi a Chi-Adventist m'Sukulu za Ukachenjede Aphunzitsira Mabuku a Chi-Evanjeliko (September 2008) – Zamveka kuti ku SAU akugwiritsa ntchito bukhu lolembedwa ndi a Charles Stanley yemwe ndi mtsogoleri wotchuka wa chi-Evanjeliko, lotchedwa Bukhu Lonyamulika la Moyo Wachikhristu [Handbook for Christin Living], m'phunziro lao la Ziphunzitso za m'Bukhu Lopatulika. Monga chodziwikiratu liri ndi ziphunzitso zolakwika pa Gehena, Zaka chikwi, Kusinthika, Chisautso Chachikuru, ndi Munthu Wokana-Khristu.

Kotale Wodzala ndi Zolakwika Waposachedwapa wa Sabata Sukulu (2008) – Kotale wa Akulu wa Sabata sukulu wachinai wa 2008, wotchedwa Chitetezero ndi Mtanda wa Khristu akuphunzitsa mosabisanso zakuti "nsembe yakutetezera machimo inathera pa mtanda" chiphunzitso cholakwika chomwe a Martin anawauza a Froom ndi a Anderson kuchilemba m'QD.

Zaka Zochuruka Zakusintha kwa Kachetechete (1960 kupita mtsogolo) – Pambuyo pakufalitsidwa kwa QD, kusintha kwakuru pa ziphunzitso kwakhala kukuchitika mwachinsinsi. Kusinthako kunalowa monyengerera kotero kuti akhristu athu ambiri sanazindikire kuti kukuchitika.

Poyamba panali kusintha komwe kunali zotsatira za zolakwika zomwe zinalembedwa m'QD. Kachiwiri kusintha kunachitika chifukwa cha kukhumudwitsidwa komwe kunachitika ndi njira zomwe bukhu la QD linalembedwera. Mungathe kudziwerengera za mbiri za chiwerengero chachikuru cha zifukwa zomwe zinadzetsa kusinthako m'mabuku omwe alembedwa kumbuyo kwa bukhu lomwe traki'yi iri chifupikitso chake.

Zinthu zitatu zosiyana zakhala zikufooketsa mpingo wathu. Choyambirira ndicho kupandukira Mulungu mwakachetechete ndi kulowerera ku za dziko m'masukulu athu a za Ukachenjede komwe kwadza chifukwa chakufuna kubvomerezeka ndi kufanana ndi maphunziro achikunja. Mbiri yakugwaku kuyambira 1911 kupita mtsogolo yalembedwa m'bukhu la mlembi wakabuku aka lotchedwa, Kusokonekera pa Cholinga [The Broken Blueprint.] Chinthu chachiwiri chinali kulolera misonkhano ndi ma-Evanjeliko ndi kulembedwa kwa QD m'zaka za ma'1950. Mbiri zonsezi zikufotokozedwa bwino m'bukhu latchulidwa'lo.

Chinthu chachitatu chomwe ndi choipitsitsa cha zonse ndicho chilakolako chakufunitsitsa kufikira magulu ambiri kwa misonkhano ya ma-Evanjeliko – chinthu chomwe chinatsegula khomo lachindunji lolowelerana ndi kubvomerezeka kwa mpingo wathu ndi mipingo ya Mpanduko, Akatolika, ndi Mipingo ya Chihelene.

Ngati wina akufuna kumvetsetsa za chiyambi cha kusemphana pa ziphunzitso pakati pathu ndi chinthu chapafupi: Angosemphanitsa kapena kusakaniza ziphunzitso ndikukhala ndi maganizo komanso chikhulupiriro chakuti ngakhale iye ali wochimwa adzalowabe kumwamba. Chodziwikanso ndi chakuti zotsatira zakulolerana ndi kuchita misonkhano ndi ma-Evanjeliko zinatsogolera atsogoleri athu kulowelera m'chiyanjano ndi mgwirizano wa Zipembedzo. Ichi chinayamba kumapeto kwa zaka za ma'1950 ndipo m'1966 magulu awiri okhawo "odzipatula amene sanali ziwalo" za bungwe la mipingo ya Dziko Lapansi [WCC], anayambanso kutumiza nthumwi zao kumisonkhano yapadera ya komiti ya ziphunzitso ku likuru kwa bungwe'li ku Geneva, Switzerland: awa anali Mipingo ya Katolika ndi Seventh-day Adventist. Kutengako mbali kwathu pa misonkhano ya WCC m'komiti yokambirana za ziphunzitso kukupitirira mpaka lero lino.

Ku kagulu ka amuna owerengeka a ku General Conference m'ma 1950, zinakhala ngati apindula chinthu china chatsopano chomwe chinatsala pang'ono kutseguka pamaso pa mpingo. Chinthu chatsopanocho chinatsegukadi – koma sichinali chomwe iwo amayembekezera.

Chenicheni chomwe chatipangitsa kuti tifooke ndicho kuchoka kwathu kwakachetechete m'Bukhu Lopatulika ndi m'Mau a Mzimu Wachinenero zomwe zakhala ziri maziko a mpingo wathu – ndi kulowelera m'misonkhano, malangizo a umunthu ndi zifupikitso za mau a chizolowezi a chikhulupiriro. Zolembera zouziridwa za Mulungu ziribenso chikoka cha kutsogolera m'malingaliro athu. Zolembera zouziridwa za Mulungu zikukanidwa kukhala nazo m'nzeru zathu.

## ZOONJEZERA – 1

## UMBONI WOPEREKEDWA NDI WANTCHITO WA GENERAL CONFERENCE (1983)

Pa nthawiyo, ndinalumikizana ndi mnzanga, amene tinadziwana pa nthawi yomwe ndimachita maphunziro anga ku Sukulu ya Ubusa ya chi-Adventist, m'Washington, D.C. kuyambira chaka cha 1955 mpaka 1958. Ndinamfunsa andiuzeko momwe wanakhala akuzionera zinthu ndi kumva pa nthawiyo kapena pambuyo pake. Dzina lake linali Ben Glanzer – amene kwa zaka zambiri, patsogolo ndiponso pambuyo pa kusokonekera kwa ziphunzitso m'ma 1950, wanakhala ali m'modzi waogwira ntchito a Bungwe la General Conference. Monga mkonzi wothandizira kulemba magazini ya Ministry komanso kukhalira limodzi ndi anzake m'GC, ku Review, ndiponso kunja ku zigawo, Ben amadziwa bwino za chomwe chimachitika m'zaka zochititsa mantha'zo.

Iye anati, "Anthu ambiri analibe chidwi ndi nthawi yowerengera mapepalawo ([manuscripts] a QD lisanasindikizidwe). Anangowabweza. Bwana wake anangopereka mapepalawo kwa mnzangayo kuti awawerenge. 'Ine ndiribe nthawi yoti nkuwawerenga. Ona chimene ungachite nao.' 'Ngati ukuganiza kuti bukhu'lo silabwno - umatsutsa chimene umadziwa chiyambi chake! Ndipo pamene ndinamuuza zomwe zinali mkati mwake, palibe chimene

akanachita. Anangotumizanso mapepala'wo komwe anachokera monga momwe anali.

"M'werengi wake (wokonza zolakwika m'zolembera za mphunzitsi wa za Mau a Mulungu ku Sukulu ya Ukachenjede ya Avondale) anafotokozera anzake za zomwe zinalembedwa, ndipo ichi chinapangitsa chidwi onse pa sukulu ponsepo.

"Pamene zolemberazo zinafika kwa a Anderson ndi a Froom anafewetsako zina ndi zina za zolemberazo. Kenaka mapepala'wo anatumizidwa ku Review kuti akayambe kulembedwa bukhu. Koma akonzi a mabuku ku Review ndi Herald sanachibvomereze ichi mofewa… Ichi ndi chifukwa chake bukhu'li liri ndi zosakanikira zambiri. Mbali ina ndi lachikunja pamene mbali ina liri bwino.

"Pakulankhula kwake iye [Martin] anatchulapo zinthu zingapo kuti ma-Adventist ayamba kuzichita mosiyana ndi pachiyambi.. Chimodzi cha izi anati ndi kuchepetsa kwa kukhulupirira Mau a Mzimu Wachinenero omwe anawatsogolera pa chiphunzitso chao.

"A R.A. Anderson anandiuza ine pamaso kuti a Froom anakana kukhuzidwa ndi zomwe zimachitikazo. Iwo anakanitsitsa zoti tikhale pa mgwirizano ndi ma-Evanjeliko. Ndipo (a Martin) anauza a Barnhouse kuti ngati angalembenso zotsutsana zina ndi ma-Adventist, 'popanda chilolezo changa, ndisiya ntchito.' A Martin anali katswiri pakalankhulidwe kao ndi mbali zonse ziwiri kuposa a Barnhouse.

"Akakhala m'misonkhano a Martin ndiwo amatsogolera..Anali ochenjera kwambiri. A Froom akalankhula chinthu mu msonkhano, a Martin amayankha powerenga zomwe [a Froom'wo] analemba m'mabuku ao zosiyanitsa ndi zomwe alankhulazo.

Chimodzi cha zifukwa zimene iwo anatumizira mapepala [Manuscripts] a bukhu'lo kwa atsogoleri akuruakuru, inali njira imodzi yofuna kuti iwonso atengeko mbali m'zomwe zimachitikazo. Panalibe aliyense anali wokonzeka kutenga umwini wa bukhu'lo.. Palibe anali wokonzeka kubvomera kuti analilemba ndiye. Mpaka pano, ambiri sakudziwa yemwe analilemba.

"Werengani kalata ya a Anderson yopita kwa a Greive ku Australia…Anderson anayankha: 'Inde, tikuyesayesa kusintha ziphunzitso, koma tikufuna tiyambe ndi abusa tisanapite kwa anthu.

" Panthawiyi a Andreasen anali atapumula ntchito ndipo amakhala pafupi ndi Loma Linda. Atsogoleri analetsa kuwapatsa a Andreasen penshoni yao chifukwa anatsutsa za QD..Kufikira pakuti mwamuna wobvutikayo anapempha ngati [ ofesi yoona osauka] ingamthandize. A ofesiyo anamfunsa, 'Sindinu m'busa wampingo wa Adventist?'.. 'Inde, koma anachotsa dzina langa,' iye anayankha. Pomwepo antchito oona za osaukawo anatuma katswiri wao wa za malamulo kuti afufuze chomwe chinachitika, mosakhalitsa a Andreasen anabwezeredwa ndikuyambanso kulandira penshoni yao kuchokera ku mpingo.

## ZOONJEZERA – 2

## UMBONI WOPEREKEDWA NDI WOPHUNZIRA ZA UBUSA (1983)

Kuchokera pa zimene anaziona wolembayu (Vance Ferrell) koyambirira kwa 1983 analemba:

"Ndinali ku Sukuru ya za Ubusa kuyambira June 1955 mpaka June 1958. Pafupifupi misonkhano yonse ya miyezi khumi, inasu ndi itatu ndi ma-Evanjeliko (March 1955-August 1956) inachitika m'nyumba ya General Conference, yomwe inayandikana kwambiri ndi Sukulu ya za Ubusayo..Nthawi yonse ndinali ndikuphunzira pa Sukulupo.

"Ndimatenga phunziro la Kumvetsetsa Chikhalidwe cha Mulungu [Systematic Theology], ndipo ndi chidziwitso chomwe chinandithandiza kumvetsetsa bwino za zomwe zimachitika.

"Kumapeto kwa nthawi yozizira ya 1955-1956, ndinalembedwa ntchito kukhala woyang'anira nyumba yonse ya General Conference yomwe inali yosanjikana magawo atatu..Sindinali woyang'anira kokha komanso mlonda.

"Oyang'anira nyumba'yi aliyense wa usiku amapatsidwa kuyang'anira gawo losiyana nthawi zonse ( gawo 1, 2 ndi 3), ine ntchito yanga imayamba nthawi ya 5 p.m, yomwenso inali yowerukira anthu onse ogwira masana, ndimatheka kugwira mozungulira zigawo zonsezo ndi cholinga chakuti a usiku anzanga naonso apumule. Ndi kagwiridwe ntchito kotereka mlungu ndi mlungu, ndimakhala ndi mwai wopezana ndi kucheza ndi ogwira ntchito amene amaweruka mochedwa.

"Pa ntchito yanga yoyambayo, ndimagwira ndekha m'zigawo zonsezo ndi kusesa m'zipinda zonse..Kenaka ndinasinthidwa, ndikuikidwa woyang'anira chigawo chapakati chokha nthawi zonse.

"Apatu ndinayamba kuchita chidwi ndi anthu owerengeka omwe amaoneka aulamuliro woposa anzao pa zomwe zimachitika m'nyumbayo'.

"Poganizira zomwe zinachitikazo, ndapeza kuti chinali chikonzero cha Mulungu kuti ndikhale woyang'anira chigawo chachiwiricho usiku uli wonse..

"M'chigawo ichi, panali chipinda chomwe chinali ofesi ya a LeRoy Edwin Froom. Pambuyo pa miyezi ingapo, ndinayamba kumapeza milumilu ya mapepala omangidwa pamodzi okula 81/2 x11. Milu imeneyi imasinthidwa pafupipafupi.. "Ndimaona mutu uli wonse wa QD uli pamwamba pa mapepala ..osanjikidwa mofanana.

"Panalibe ofesi ina momwe mumapezeka milu ya mapepala a bukhu'li m'General Conference.. Ndinalinso nditauzidwa kale kuti a Froom amalemba ndiponso kuchita zofufuzafufuza okha ku nyumba kwao ku Takoma Park. Mu nyengo yamphukira ya 1956, zotsatira za misonkhano ya a Martin-Barnhouse zinayamba kuonekera. Tikamaphunzira m'makalasi a Sukulu ya za Ubusayo, pamakhala kupereka ndemanga za chikhalidwe cha Khristu, zomwe zimakhalako zomverera kuposa za nsembe yakutetezera kuti inathera pa Gologotha komanso za kugwirizana kwa Mzimu Wachinenero ndi ziphunzitso za chikhulupiriro chathu..

"Zimaoneka kuti aphunzitsi pa Sukulupo amadziwapo kanthu za chiphunzitso china chatsopano..

"Pa nthawi yokhayokhayo pomwe zimanenedwa za kuthera pa mtanda kwa chitetezero, tinayambanso kuuzidwa kuti Ellen White sanachitepo chiri chonse, m'njira ina iri yonse, za kukhazikitsidwa kwa ziphunzitso za chi-Seventh-day Adventist.. Apa ndinatsutsa kuposa wina ali yense m'kalasimo za chiphunzitso cha chilendochi.

"Zimatheka maiyu kutengedwa m'masomphenya ndi kusiya kuganiza osadziwa chomwe chimamchitikira akamalandira ziphunzitso zomwe amapatsidwa, ndipo amuna onse amene amakhalapo pa "Misonkhano ya la Sabatayo" amagwirizana nazo ndi kutsimikizika pa chiphunzitso chiri chonse..

"Zimatheka kukhala ngati wakomoka kotero kuti abale'wo anafika pokhala ndi chitsimikizo chakuti chiri chonse chimene anawauza pamene iwo anasokonekera pa chiphunzitso, amachikhulupirira kuti chinali chochokera mwachindunji kwa Mulungu, osati m'maganizo ake.. Pa nthawi imeneyi amatengedwa iye mu mzimu – akatsitsimuka nkumawapatsa kumasulira kokhoza pa zomwe iwo amakambirana. Izi zinachitika kawirikawiri. –Anali Mulungu wakumwamba kudzera mu Mzimu Wachinenero yemwe amatipatsa ziphunzitso zathu kapena kutitsimikizira kuti zinali zoona.

"Panalinso mphekesera yokhuza za kumvera lamulo la Mulungu kuti pali 'chisonyezo chakuti wolisunga ndi okhawo omwe alandira kale chipulumutso.' Chikhalirecho chipulumutso sichimaperekedwa pamene munthu wangotembenuka, ndiponso popanda kumvera lamulo la Mulungu.

"Panali madzulo ena omwe sindikuwayiwala.

"[Ndinali kusesa ndi kupukuta m' Ofesi ya a Froom pamene ndinaona kalata yotsegula itaikidwa bwino, pakatikati pa tebulo limene nthawi zambiri limakhala lopanda kanthu.. Ndipo zikuoneka kuti inaikidwa mwadala kuti indikope ndikuiwerenga.

"Imafotokoza za mtsikana wina yemwe anangotembenuka kumene ndi kubatizidwa chifukwa cha uthenga wa chi-Adventist. Bambo ndi mai wake, atamva, anali okhumudwa kwambiri. Ndipo anamlembera m'modzi wa chi-Evanjeliko cha Mpatuko Dr. Bonald Grey Barnhouse.. Namuuza iye za chokhumudwitsa chimene chinamchitikira mwana wao ndikumpempha mkuruyo kuti athandizepo..

"Dr. Barnhouse anayankha powalemberanso kalata.. Anawafotokozera makolo'wo kuti iye ndi Dr. Martin anali mkati mwa ntchito yowatembenuza ma-Adventist kuti agwirizane ndi chi-Evanjeliko cha Mpatuko – pakusintha ziphunzitso zao. Ndipo anatsimikizira banja'lo kuti iye ndi a Martin agonjetsa..

"Makolo'wo anasonyeza kalata ya a Barnhouseyo kwa mwana wao, ndi chiyembekezo chakuti imulimbikitse kubwerera ku mpingo wa makolo'wo.. Mokhumudwa kwambiri mtsikanayo anatenga kalatayo ndi kuipereka kwa mbusa wa chi-Adventist. Ndipo kalata inali m'dzanja langayo-yomwe imafotokoza za izi-inali yotumizikwa kwa a L.E. Froom kuchokera kwa mbusa wa mpingo wathu.

"Pamodzi ndi kalatayo panalinso kalata inanso yolembedwa pa taipi yomwe a Barnhouse anatumizira makolo a mtsikanayo. Ndinaiwerenga iyonso.. Kalata ya a Barnhouseyo inaikidwa mosamalitsa kunsi kwa kalata yomwe inali pa pamwambayo.

"Pamene, ndinanyamula katata ya a Barnhouseyo ndinaonanso kuti kunsi kwake kunalinso kalata ina..yolembedwa ndi kusainidwa ndi a Froom, kalata yachitatuyi inali yopita kwa a Barnhouse..

"Iwo [a Froom] analemba kalatayi kuwatsimikizira a Barnhouse kuti zinthu zonse zinali bwino..

"Simunandiyankhe pa zinthu zina zomwe ndinakufunsani. Pali zobvuta zina zomwe ndikumva za izo. Si kuti ndikukukaikirani ai. Koma chokhacho choti simukundiyankha chandipangitsa kudabwa.'

"Makalata awiriwa anaulura chifukwa chenicheni chimene a Martin ndi a Barnhouse anakhuzidwira kwambiri ndi misonkhano imachitikayo. Cholinga chao sichinali kungolemba bukhu; a Martin amadziwa bwino chomwe chinali cholinga chowabweretsa pamodzi a Barnhouse ndi atsogoleri a maudindo apamwamba kwambiri a chi-Adventist kuzokambirana zomwe zinatha nthawi yoposa zaka ziwiri. Cholinga chao chinali kuutembenuza mpingo wonse.

"Zikanakhala kuti a Froom anali limodzi nao pazochitika zomwe amunawa amazilingalira, sakanayankha kalatayo momwe anachitira.

"Ndikukumbikira bwino ndithu – chifukwa chinthu ichi chinali chodzidzimutsa m'moyo wanga – kuti sipanathe mlungu umodzi

kuchokera pomwe ndinawerenga kalata ija, kuti ndinakhala m'malo opempherera a Sukulu ya Ubusayo [ momwe a Froom anadzatilankhula]: 'Kuyambira pomwe ndinayamba kuwadziwa a Barnhouse, ndinalibe chifukwa chakuti nkukaikira zolinga zao..'" Sindidzaiwala zomwe ndangokuzani pasachedwazi.. Chinali chifuniro cha Mulungu, kuti makalata aja apezeke pa tebulo paja usiku uja. Ndipo zoonadi ndikuchiona kukhala chosayenera kuti ndikhale chete za awa pano, patapita zaka zambiri..

"Linali bvumbulutso kumva bambo Martin kuchokera pakamwa pao. Pamene analankhula, mau ao oturuka ngati zipolopolo zoombedwa mwamphamvu..

"Iwo amalalikira kuchokera pa Machitidwe 17:23. Ndi mau ngati a munthu wochita zisudzo analiuza gulu linasonkhana'lo m'mawa umenewo za Artene amene mosadziwa anapembedza Mulungu wosadziwika. Pamenepo iwo anati, mau'wa anazokotedwa, 'Kwa Mulungu Wosadziwikayo.' Iye amene mumpembedza wosamdziwa; Iye amene ndilalikira za Iye kwa inu!' Ndipo mosamalitsa analankhula za chipulumutso chochitika mwa chisomo basi..

"A Walter Martin anali amsinkhu wa zaka za mkatikati mwa makumi asanu, ndipo pomwe anali kutsogolera Misonkhano ndi Ma-Evanjeliko anali chimunthu chazitho zao ndi a chikoka. Pamene iwo analankhula za 'umodzi,' anatanthauza kugonjera..

"Uyu ndi mwamuna amene anatsogolera m'misonkhano ndi atsogoleri a chi-Adventist, kuyambira nyengo ya mphukira 1955 mpaka dzinja 1956. Uyu ndi mwamuna amene bukhu Mafunso Pa Chiphunzitso [QD] linalembedwa kumkondweretsa."

## ZOONJEZERA – 3

## KUSOKERETSA KWA ZIPHUNZITSO ZA *M'QD* NDI SDAB

Za thupi la Umunthu la Khristu – Pamene Khristu anadza ku dziko lapansi anatenga thupi lathu la umunthu la uchimo'li. Chokondweretsa nthawi zonse kwa mlembi yuno ndi chakuti Mau a Mzimu Wachinenero akufotokoza momveka bwino za thupi la umunthu la Khristu; ndipo mkangano pa nkhaniyi sunachitikepo kufikira patadutsa zaka zambiri chifere amai White.

Mafotokozedwe awiri omwe anthu amakanganirapo:

"Yesu analora umunthu pamene mtundu wa anthu unali chifookere ndi uchimo kwa zaka zikwi zinai.. Iye anadza m'thupi lotere'li kudzagawana nafe zisoni ndi mayesero, ndikutipatsa ife chitsanzo chakukhala moyo womvera ndi wachiyero.

"Satana anakutenga kuchimwa kwa Adamu kuti ndi chitsimikizo chakuti lamulo la Mulungu linalibe chilungamo choncho kunali kosatheka kulisunga. Khristu anadza m'chikhalidwe chathu, kudzapulumutsa kulephera kwa Adamu.. Pakuti kwa zaka zikwi zinai mtundu wa anthu unakhala ukufokerafokera ku thupi, m'nzeru ndiponso moyo wauzimu; choncho Khristu anadzitengera pa Mwini yekha zifooko za umunthu wakugwawu. Pakutero Iye anaombola onse kuchokera madera akunsi komwe munthu anagwerako.

"Ambiri amati kunali kosatheka kuti Khristu achimwe... Ngati ife tingagwe m'mayesero kuposa amene Khristu anakumana nawo, ndiye kuti sayenera Iye kukhala Mpulumutsi wathu. Koma Mpulumutsi wathu anatenga umunthu ndi zifooko zake zonse. Iye anatenga thupi la umunthu, lomwe likanatha kugonjera ku mayesero."

"Iye ali chitsanzo chathu ndipo, mwa chikhulupiriro chathu mwa Iye, ifenso tiyenera kugonjetsa pa yesero liri lonse ndi kukhala olakika."

"Zoona?" Nanga ndi chifukwa chiyani iwo okhotetsa chiphunzitso cha mau a Mulungu'wa – pamodzi ndi ma-Evanjeliko – akukana choonadi ichi? Chifukwa chakuti akulimva kukoma tchimo ndiye akufuna adzingokhala momwemo kufikira imfa yao.

Iwo amatsutsana ndi ziphunzitso zina zonse, mwachitsanzo za chabwino ndi choipa monga zikupezeka mu QD ndi SDAB ponena za thupi la umunthu limene Khristu analitenga pamene anadza ku dziko lapansi.. Tiyeni titsutsane ndi chiphunzitso chiri chonse cholakwika chomwe chingapezeke m'mabuku a ziphunzitso zobvomerezeka a chi-Adventist.

Kafotokozedwe kolakwika ka umunthu wa Khristu m'QD: "Ngakhale anabadwa m'thupi, Iye [Khristu] m'njira iriyonse anali Mulungu, ndipo sanatengeko chiri chonse cha zoyamwira cha umunthu kuphatikiza zilakolako, chidetso zomwe zimadzetsa ufooko wa ana a Adamu. Anali 'wopanda tchimo,' osati m'machitidwe akunja okha, koma m'chikhalidwe chake chonse."

"Koma ngakhale wosachimwa m'moyo wake ndi chikhalidwe chake.."

"Inde, sizingatheke kunena.. Yesu sanadwalepo kapena kuti sanamvepo zifooko zomwe matupi athu a uchimo'wa amazimva. Iye anakomana nazo zonse'zi. Iyetu anasenza zonse'zi m'malo mwa ife.

"Zonse'zi, zifooko, kubuula, zolemetsa ndi zolephera timazisenza ife m'matupi athu ochimwa ndi akugwawa. Kwa ife izi ndi mbali ya chilengedwe, ndi zotengera kwa makolo athu, kotero kuti pamene Iye anasenza izi, anatero osati chifukwa chakuti anali wofooka.. Iye anazisenza izi mu ungwiro wake, ndi m'chikhalidwe chake chopanda tchimo. Yesu anasenza zonse'zi chifukwa cha ife. "Zonse zimene Khristu anasenza.. anatero chifukwa cha ife.

Chikhalidwe cha thupi la umunthu la Khristu molingana ndi bukhu la SDAB:

".. koma Iye analibe chifooko chotengera kuchokera ku umunthu." Malingana ndi mau awa zikutanthauza kuti Yesu anatengera umunthu wathu wa thupi, koma osati chifooko cha uzimu. Iye sanatenge umunthu wonse wathu wakugwa'wu.

"Iye anatenga chikhalidwe cha umunthu wakugwa'wu…osati chakusayeruzika."

Mau otsutsana chomwechi'wa amapezeka m'chiganizo chimodzi ndipo zili choncho chifukwa chakuti mabuku'wa anakhala akukonzedwa ndi akonzi osiyanasiyana asanasindikizidwe.

Za Chitetezero – Zakuti ntchito yakutetezera inathera pa mtanda, ndicho chiphunzitso cha mitu ya m'QD:

"Mukangokhulupirira pomwepo mwapulumutsidwa," ndi mau omwe amalalikidwa ndi onse. Koma choonadi chake ndi chakuti ngati ife sitingalumikizane, ndi kudalira m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku pa Khristu ndiponso pa Mulungu mu ntchito yake ya chipulumutso chathu, sitingapulumutsidwe.

"Mosachita kukaika nsembe yonse yakupulumutsa ya Yesu Ambuye wathu inathera pa mtanda." Pachiyambi liu lomwe limagwiritsidwa ntchito linali "chitetezero." Koma akonzi analisintha kukhala "nsembe yakutetezera." Palibe pali ponse m'QD pomwe pakupezeka liu chitetezero litagwiritsidwa ntchito za utumiki wakutetezera womwe ukuchitika pano pambuyo pa imfa ya pamtanda.

"Tikukhulupirira kuti nsembe ya machimo ya pa mtanda ndi yokwanira, yangwiro yochotsa machimo,. Ikukwaniritsa zofunikira zonse [za chipulumutso]." "Choncho wina akamamva m'Adventist, kapena kuwerenga m'zolembera za chi-Adventist – ngakhale m'zolembera za Ellen G. White – kuti Khristu akutitetezera pano, ayenera kumvetsetsa kuti timatanthauza kuti Khristuyo panopa akugwiritsabe ntchito ziyenerezo zonse za nsembe yakukhululukira machimo imene anaichita pa mtanda."

"Nsembe iyi [ya pa Gologotha] inali yokwanira. Inapereka chitetezero ku mtundu wonse wa anthu."

"Koma sinali ndi chiyembekezo chotipezera china chake pa nthawi ija, kapena nthawi yamtsogolo. Palibe! Iye anatipezera kale ichi pa mtanda."

QD likugwiritsa ntchito mau, "nsembe yakuchotsa;" awa kwenikweni akutanthauza kuti imfa ya Khristu pa Gologotha inali yongochotsa pamene "zotsatira zake" zangokhala zongogwiritsidwa ntchito pambuyo. Kodi zotsatirazo ndi chiyani? Kukhululukira machimo kokha.

Bukhu la ziphunzitso la 1988 la SDAB, likuphunzitsa ganizo lolakwika lomwelo: Ilonso limati kukhululukira machimo kunathera pa mtanda:

"Mau ake akupfuula 'Kwatha" anaimira kutsiriza kwa ntchito yake."

"Kukhululukira kapena kuti kuyanjanitsidwa, kunathera pa mtanda..wokhulupirira wolapa kotheratu angathe kungokhulupirira mu ntchito yotsirizidwayo."

"Utumiki waumkhalapati wa Khristu woukayo kwa akufa uli m'magawo awiri lakukhululukira ndi la kubveka.. Liu la pa Gologotha 'Kwatha' limaimira (kutsirizika)."

Chodziwika ndi chakuti, m'bukhu ili lobvomerezeka la ziphunzitso za chi-Adventist, muli zolakwika zonse'zi ndipo zidzapitirira kutero. Mau a Mzimu Wachinenero akutiuza kuti Satana amachita chipambano pamene amatha mosabvuta kusakaniza choonadi ndi bodza. Choopsya chachikuru m'mabuku onse'wa ndicho kugona tulo kumene akhristu tirimo kosati ndi kumvera nako.

A George Knight, m'mau ao[omasulira QD la 2003] lomwe linasindikidwanso mobwerezabwereza akufotokoza kuti bukhu'li likuphunzitsa chiphunzitso chokhoza za chikhululukiro chathu. Koma choopsya chomwe chiri m'bukhu'li, ngakhale limalimbikitsa za chikhululukiro, ndichakuti silimalimbikitsa za kufunikira kwa kumvera malamulo a Mulungu. Pafupifupi mpfundo zonse zofunikira, monga zaperekedwa m'mitu 23-24, ndi 28 ya Bukhu la Great Controversy (pp 409-432, 479-491) mulibe m'QD! Ichi n'chifukwa chakuti izi zikuonetsa kuti tiri ndi mbali yakuchitapo pa chipulumutso chathu yomwe ndi kukhala omvera.

QD silikunenapo chiri chonse za mphamvu yakukhala womvera imene Khristu amapatsa kwa ophunzira ake! Likungophunzitsa za kukhululukira, kukhululukira, kukhululukira! Misonkhano ndi ma-Evanjeliko ndi QD, bukhu lomwe linali chotsatira chake, ndizo magwero awiri omwe kunachokera kupandukira kwathu pa ziphunzitso. Gwero lina lafotokozedwa m'bukhu langa, Broken Blueprint.

Mkati mwa ndime zoposera makumi awiri ndi zinai za m'QD zomwe zikulankhula za chikhululukiro, ndinangopezamo imodzi yokha yomwe ikupereka uthenga wokhoza. Koma kuti mupeze uthenga wokhozetsetsa ndi wokuthandizani kumvetsetsa za chitetezero ndiponso Kachisi wakumwamba, umene simungaupeze pali ponse, werengani Great Controversy, mitu, 23, 24 ndi 28.

Za Kachisi wokhala ndi Zipinda Ziwiri m'Mwamba – Chiphunzitso cha Kachisi wokhala ndi zipinda ziwiri m'Mwamba chimadedwa kwambiri ndi anthu omwe amakhulupirira ziphunzitso za umunthu. Iwo amafuna adzimva kuti Khristu analowa m'chipinda chimodzi, Malo Opatulikitsa (chomwe amaganiza kuti ndiko kumwamba'ko), komwe palibe chomwe Iye akuchita.

M'bukhu la QD palibe pali ponse likutchulapo za zipinda ziwirizi, ndiponso chiri chonse chokhuzana ndi chomangidwa kumwamba. M'bukhu lotsatira la ziphun-

zitso, la SDAB nalonso likungotsindika za chikhulululukiro. Mulibe liu ndi limodzi lomwe likutchulapo za mphamvu yakulimbikitsa kulikana ndi kuligonjetsa tchimo.

Za Chiweruzo Chakufufuza – M'QD mulibe pena pali ponse pomwe pakutchulidwapo za chiweruzo chakufufuza.. "Zipinda" ziwiri za kachisi wapansi pano zimangotanthuza "magawo" awiri a ntchito ya Khristu kumwamba osati zipinda zeni-zeni ziwiri:

QD: "Utumiki uwu waukuruwansembe wa Ambuye wathu, tikukhulupirira, uli mapeto a ntchito ya chiweruzo..Iye samatumikira 'm'malo omangidwa ndi manja'..mautumiki amitundu iwiri amachitika m'kachisi wakale – woyamba, wakuyanjanitsa m'chipinda chopatulika, ndipo wachiwiri, wa chiweruzo m'chipinda chopatulikitsa – kuimira mautumiki magawo awiri a utumiki wa Ambuye monga Mkuruwansembe." "…gawo lotsiriza la utumiki womwe tikuudziwa kuti ndi ntchito ya chiweruzo.." "..tsiku la chiweruzo.. ntchito ya chiweruzo."

Tikugwirizana nazo kotheratu kuti chiweruzo chakufufuza chikukhuzana ndi ntchito ya chiweruzo – komanso ndi nthawi imene anthu a Mulungu pa dziko lapansi pano ayenera kuchoka m'machimo ao, ndikufunitsitsa kukhala olungama! Ganizo lomwe likukanidwiratu m'QD.

Kwa a Froom Gologotha anakwaniritsa zonse; palibe china chinatsalira kupatula chikhulululukiro. Pamene anali nkufotokoza ichi, kwa iye hagia, limatanthauza kuti Yesu analowa m'zipinda zonse zopatulika mu A.D. 31, ndipo chotsatira chinali chifundo ndi chikhulululukiro. "Yesu analowa 'm'malo onse opatulika,'.. Koma osati ndi chiyembekezo chochitapo kanthu kena kali konse m'malo mwathu pa nthawi iyi [pambuyo polowa m'Kachisi], kapena m'tsogolo. Ai! Anatipulumutsa kale pa mtanda."

QD: "Nsembe [ya pa Gologotha] ndi yokwanira m'zonse, yangwiro, yakuchotsa tchimo, yomwe ikukwaniritsa chiyero cha Mulungu ndiponso zofunikira zonse, ndi cholinga chakuti, chifundo, chisomo ndi chikhulululukiro zipatsidwe kwa munthu wochimwa, popanda kudetsa chiyero ndiponso kutsitsa mbendera za Mulungu ndi ulamuliro wake."

Tanthauza la mau [alembedwa pa mwambawa], ndi lakuti Mulungu angathe kulora ochimwa kulowa kumwamba, popanda kudetsa boma lake. Chofunika ndi kungolapa ndi kukhululukidwa!

QD: "Kuti munthu apulumutsidwe, chingofunika chikhulululukiro!

"Pakupereka nsembe za m'mawa ndi madzulo, iwo [a Israyeli] amatsimikizika kuti machimo ao akhululukidwa.

"Wochimwa ali yense pa yekha palibe chomwe angachite. Nsembe zimaperekedwa m'malo mwa iye, kaya amafuna chikhulululukiro kapena ai."

Palibe liu ndi limodzi lomwe likutchulidwa [m'QD] lokhuza za kufunikira kwa kulapa ndi kusiya machimo m'miyoyo ya ochimwa kuti machimo achotsedwe! Molingana ndi a Froom, machimo ochotsedwa kwa munthu ndi omwe adzakhululukidwa, koma osati chifukwa chakuti iye wawasiya.

Chiphunzitso cha umunthu chimati chiweruzo cha kufufuza pa Danieli 8:14 chikungokhuza za kuweruzidwa kwa kanyanga kakang'ono. Ngakhale kulakwika uku sikukupezeka m'QD, a George Knight alemba m'zolembera zao zoonjezera m'QD limene langosindikizidwanso:

'Kuyeretsanso' kapena chiweruzo cha pa Danieli 8:14 chikunena za kanyanga kakang'ono osati anthu a Mulungu.

Malingana ndi chiphunzitso cha umunthu, chiweruzo cha kufufuza ndi kuweruzidwa kwa ulamuliro wa kanyanga kakang'ono "kusanachitike kudza-kwachiwiri." Sichakufufuza m'miyoyo kapena kuona kumvera kwa anthu a Mulungu. Kumasulira monga komweku kukupezekanso (m'bukhu lotsatira, la SDAB) momwe akupitiriza kuti m'chiweruzo chimenechi mudzakhala mulibe kutetezera, koma ntchito yokhayo ya kuweruzidwa kwa kanyanga kakang'ono.

"Masomphenya a Danieli'wa akunena za chiweruzo momwe Mulungu adzapereka chilango kwa kanyanga kakang'ono pakudza kwachiwiri kusanachitike."

"M'chiweruzo ichi chidzaperekedwa chilango ku ulamuliro wopandukira Mulungu wa kanyanga kakang'ono, chidzaperekedwa 'chifukwa kanazunza oyera mtima a Wam'mwambamwamba.'"

Za Kuyeretsedwa – M'bukhu latsopano [SDAB] kuyeretsedwa kukuchitika popanda ife kuchitapo chiri chonse, popanda ife kutengapo mbali pakumvera, koma mwa "chisomo " cha Khristu.

"Ambiri akuganiza molakwika kuti kubvomerezeka kapena kukanidwa kwao pamaso pa Mulungu kudalira pantchito zao zabwino kapena zoipa..

"Sizoona kuti kuyenerezedwa ndi kuyeretsedwa kuli zotsatira za ntchito za mtundu uli wonse."

Pa tsamba 123 wowerenga akuuzidwa kuti pamene wochimwa choyamba adza kwa Khristu, nthawi yomweyo amayeretsedwa ndi kuomboledwa (kupulumutsidwa). Pambuyo pake, amatsatidwa ndi mayeretsedwe a mitundu iwiri oonjezera."

"Mayeretsedwe a magawo atatu'wo ndi awa:

1) kumva kuperewera kwa moyo wakale wawokhulupirira;

2) zochitika m'moyo watsopano wawokhulupirira;

3) zotsatira zotsiriza zomwe wokhulupirira amazimva chifukwa chakuyanjananso kwake ndi Khristu...pa nthawi yakuyenerezedwa wokhulupirira amayeretsedwanso..Iye amakhala 'woyera.' Akafika pamenepo wokhulupirira mwatsopanoyo amapulumutsidwa..ndikukhala kotheratu m'manja mwa Mulungu.

"Machitidwe akulapa kotheratu" amatsatidwa ndi kuyeretsedwa kwa moyo wakale wawokhulupirira ndipo nthawi yomweyo amatsatidwa ndi chipulumutso ndikukhala m'manja mwa Mulungu. Chiphunzitso cha machitidwe akuyeretsedwa ndi kupulumutsidwa kwa msangamsanga'chi, ndi chachilendo ku ziphunzitso za Bukhu Lopatulika ndi zolembera za Mzimu Wachinenero.

Gawo lachiwiri'li zokaikitsa?? –tsamba 206.

Gawo lachitatu lakuyeretsedwa ndilongopeka monga lirinso loyamba.

A Gulley akufotokoza kuti tidzalandira "kuyeretsedwa" kwatsopano pakubwera kwa Yesu. Choonadi n'chakuti, pakubwera kwachiwiri kwa Khristu, oyera mtima adzasinthika; sikuti adzayeretsedwa! Chimene chikulakwika m'chiphunzitso cha umunthu'chi ndi chakuti amanena kuti timapulumutsidwa tikangotembenuka mtima ndipo tikatero timakhala "oyera"nthawi zonse.

Za Kumvera – Chiphunzitso chogarukira Mulungu cha makono cha mipingo ya Mpanduko chimati sitiyenera kusunga malamulo a Mulungu (chifukwa Yesu akusunga malamulo'wo m'malo mwathu), sitingathe kumvera malamulo (chifukwa tiri m'chakwaipa chakubadwa nacho), ndipo Iye sakufuna kuti tiyesere kusunga malamulo ake'wo (chifukwa anathetsedwa). Kumvera ndi "mchitidwe" umene udzabwera wokha mwa chisomo kwa ife.

QD: "Tapulumutsidwa ndi chisomo chokha." "Titapulumutsidwa choncho.. zofuna za lamulo zikukwanitsidwa." Kuchita bwino, kugwirizana ndi malamulo a Mulungu, ndikukwanitsa zonse zimene akunena.. sikunapulumutsepo moyo."

Palibe liu ndi limodzi m'QD lomwe likutchulapo za tchimo ndikufunikira kwakulisasa. Bukhu lotsatira [SDAB] nalonso likupondereza zakufunikira kwakuti munthu alimbane ndi mayesero ndiponso machimo a mkati mwake. Choonadi chikanenedwa theka, chimakhala choonadi chatheka.

"Chipulumutso ndi mphatso." "Mulungu anamasula anthu ake kutchoka m'chilango ndi themberero la tchimo."

"Akhristu sasunga malamulo kuti alandire chipulumutso – Onse amene angayesere kutero adzapezeka ali pansi paukapolo wa tchimo."

Chiphunzitso chatsopano cha umunthu chimakutenga kumvera kukhala chotsatira cha kupulumutsidwa komwe kwachitika kale, popanda chiyanjano cha mtundu uli wonse ndi Mulungu. Chiphunzitso'chi chimachitenga chipulumutso kukhala chinthu choyamba (chochitika nthawi ya kutembenuka mtima) ndi ntchito zabwino ngati zingachitidwe, monga zotsatira. Choncho wotembenuka aliyense asadandaule ngati izi zichitika kapena ai.

Za Kukhala Wangwiro - Ungwiro m'khalidwe ndiko kumvera ndi kuchita malamulo a Mulungu. Ichi ndicho cholinga chomwe tonse tiyenera kuchifunitsitsa kosalekeza.

Anthu onse ogwiritsitsa chiphunzitso cha umunthu amalitenga liu ungwiro kutanthauza kukhwima m'khalidwe la umunthu. Iwo samatchulapo za kufunikira kwa kumvera ndi kusunga malamulo a Mulungu.

SDAB: "M'Chipangano Chatsopano, ungwiro ukutanthauza anthu wokhwima..m'uzimu, m'nzeru, ndi mu mphamvu za thupi."

Mzimu Woyera amachichita ichi..Mwa chikhulupiriro. "Ungwiro ndi mphatso."

Koma ife tikunenetsa kuti palibe munthu angakhale wangwiro popanda Khristu, koma ungwirowo si chinthu chomwe chimapatsidwa kwa ife kwa ulere, popanda ife kuchitapo kanthu komwe kuli kuulandira.



(Uthengawu ukufalikira dzko lonse. MOSCOW Pamwambapa)

Za Chipulumutso – Chiphunzitso cha umunthu chimati chipulumutso chimadza munthu akangotembenuka. Ali yense amene angawerenge ndime iyi kuchokera m'SDAB akuuzidwa kuti chipulumutso chiri m'mitundu iwiri: choyamba, ndi chipulumutso chomwe chinachitika pa mtanda; ndipo chachiwiri chidzachitikanso pakubwera kwachiwiri kwa Yesu, kotero kuti ngakhale akhristu adzichimwa m'nthawi yapakatiyi anapulumutsidwa kale. Mlembi wa bukhu'li akuyesetsa kuchipinda choonadi cha Bukhu Lopatulika kuti ife tikhulupirire kuti chipulumutso chathu chiri kutsogolo.

"Chiphunzitso chakuti Bukhu Lopatulika likuti kumbali ina kuli umwana ndi kuomboledwa – kapena kuti kupulumutsidwa – kutanthauza kuti 'chipulumutso chinakonzedweratu' kale ndipo kuti, m'mau ena, kwa ena sichinachitike, ndi chongosokoneza anthu. Chidziwitso cha ntchito yonse ya Khristu monga Mpulumutsi chimapereka yankho. [Mphunzitsi wa Sukulu ya Ubusa wa chi-Adventist akufotokoza:] 'Paulo analumikiza chipulumutso chathu cha nthawi ino ndi kubwera koyamba kwa Khristu. Mu nthano ya mtanda, kuuka kwa akufa, ndi utumiki wam'mwamba za Khristu, kulungamitsidwa ndi kuyeretsedwa kwathu zikwanitsidwa




kwa muyaya. Za chipulumutso chathu cha mtsogolo, kubvekedwa ulemelero kwa matupi atsopano, Paulo anakulumikiza, ndi kubwera kwachiwiri kwa Khristu.

"Paulo akunena motsatizana.. chipulumutso chatsopano..chipulumutso chamtsogolo." Chatsopano [chinatsirizidwa kale] ndi Chamtsogolo [chidzatsirizidwa mtsogolo] ndi ziphunzitso zopekedwa chabe ndi ma-Jezuiti. Chiphunzitso cha umunthu za chipulumutso chimaphatikiza zipulumutso za mitundu yonse chatsopano ndi chamtsogolo. Chimati moyo wanu unapulumutsidwa kale "pa nsembe yomwe inathera" pa mtanda. Chofunika ndikungochilandira ichi. Malingaliro ndi thupi zanu zidzakhalabe m'machimo amene mwakhala m'kuwachita mwa chizolowezi kufikira Kubwera Kwachiwiri pomwe machimo'wo adzachotsedwa mozizwitsa. Pano chofunika kuchichita ife ndicho kumlora Mzimu Woyera mosazengereza kuti alowe ndikugwira ntchito m'moyo wathu, popanda kulimbana naye kapena kulimbana ndi uchimo ku mbali yathu.

"Mzimu Woyera amabweretsa "Kwatha" wa pa Gologotha m'moyo, pogwiritsa ntchito machitidwe okhawo a Mulungu oulandira umunthu wathu. "Kwatha" uyu wa pa mtanda amakhuza zochimwa zonse munthu amazilakalaka…"

Malingana ndi ndime yapamwambayi, zikuoneka kuti munthu sayenera kudza mwa chikhulupiriro kwa Khristu, sayeneranso kumvera lamulo liri lonse la Mulungu. Machitidwe ali wonse otero safunika ngakhale pang'ono.

# M'MISONKHANO NDI MA-EVANJELIKO

## ZOONJEZERA – 4

## ZIPHUNZITSO ZOLAKWIKA M'KOTALE NDI BUKHU ZA GULLEY

Zifupikitso: COS = Bukhu la 1982 la a Norman Gulley, Christ Our Substitute/3SSQ = The Senior Sabbath School Quarterly wa kota ya chitatu, 1983, zolembedwa ndi a Norman Gulley, mlembi wosankhidwa ndi General Conference kuti alembe bukhu la Seventh-day Adventists Believe, la 1988. Ngakhale kunali kosayenera kutero, koma a Norman ndiwo anasankhidwa kulemba zolembera zoyambirira za Seventh-day Adventist Belive.

Chiphunzitso cha a Gulley za Umunthu wa Khristu – "Khristu anatenga uzimu wa munthu asanachimwe ndi thupi la umunthu pambuyo pa kuchimwa."

"Chiphunzitso chiri chonse chakuti kudzera mkubadwa kwake Iye anakhala chimodzimodzi ngati ife, kuphatikiza umunthu wathu wa uchimo'wu, nalandira izi mwachibadwa ndi bodza lalikuru – ndipo kukhala nkhoswe kwake ya ife ndikokaikitsa.

"Khristu anatipulumutsa ife mu mphamvu ya umulungu wake yokha, yomwe inaupanga umunthu wake kukhala wangwiro.

"Yesu sanadze chifukwa chakufuna umunthu wangwiro. Umulungu wake unali wokwanira."

Choncho, molingana ndi ndime iri pamwamba'yi, Khristu anatenga umunthu wa mitundu iwiri ndi kutipulumutsa ife kudzera mu umulungu wake osati chifukwa cha umunthu wake. Kuphatikiza pa ichi, iye akuima pakuti mwachilengedwe tchimo timachita kubadwa nalo pa moyo wathu: "Sipakuchita choipa chiri chonse kuti timakhala ochimwa. Koma tinabadwa ochimwa.

Pa za Chitetezero Gulley amati – "Kwatha" anamveka ku miyamba yonse kuyambira kale ndi mtsogolo m'mbiri ya dziko..chipulumutso chake (cha munthu) chinathera pa mtanda pa Friday."

Kumapeto kwa COS a Gulley alemba zochokera m'maganizo mwao m'njira ya zokambirana pakati pa wophunzira ndi "Bob" yemwe akuyankha:

[Q] 'Kodi Iye [Khristu] akufunikanso kuonjezera china chake pa nsembe yomwe anaipereka? Kodi mau akuti "kwatha" pa Gologotha anali abodza?

[A] 'Liu "Kwatha' likutanthauza kuti zonse nkhondo [yaikuru] ndi chipulumutso cha munthu zinatsirizika.

[Q] 'Kodi utumiki wa Khrsistu pambuyo pakuuka kwa akufa, ukuonjezeranso chiri chonse pa zomwe zinachitika pa mtanda, monga tinene kuti nsembe ya pamtandayo sinakwanire? Bob anamwetulira, "Ayi."

Choncho malingana ndi Gulley, ntchito ya Khristu m'Kachisi wakumwamba ndi yosafunikira.

A Gulley pa Kachisi wa Zipinda Ziwiri – A Gulley anaphunzitsa wophunzira wao kuti: "chiphiphiritso cha Kachisi chinali chothandizira.. kumveketsa cheni cheni chomwe Kachisi ali – kaya kumwamba kweni kwakeko kapena china chake chongoimiridwa ndi wa padziko lapansi uja.'

Ngakhale a Ellen White akufotokoza momveka bwino, wophunzirayu akuoneka kuti sakumvetsetsa konse! Werengani Great Controversy, mutu 23.

A Gulley pa za Kumvera – "Khristu anapereka dipo la chipulumutso chathu nkosafunika kuti ife tichitenso kanthu kapena chiri chonse kumbali yathu." "tingofika mwachikhulupiriro ndi kuchilandira ichi." "Mbali yathu kuti tichilandire ichi ndiyo kubvomera kuomboledwa." "Ntchito ziri zonse sizingatiyenereze.. kulungamitsidwa ndi chipulumutso ndi mphatso za ulere za Khristu."

A Gulley pa Chiweruzo Chakufufuza – A Gulley aonetsera m'kwiyo wao mkayankhidwe ka "ophunzira" ao: "Ndimaipidwa ndikamaganizira za ichi." 'Chiweruzo chachiyaninso pamene pali zizindikro zochuruka za chikondi?' Iye anaomba m'manja mwake mwamphamvu. "Ndikunyansidwa ndi chiphunzitso ichi! Lupanga ili lokhala nthawi zonse pa khosi pathu!

A "Bob" ayankha, Chiphunzitso ichi cha-patsogolo pakubweranso ndi chongofuna kutsimikiza ngati iwo amene aitanidwa ailandiranso mphatso yaulereyi. Pakuti si ntchito zathu zomwe zingatiyenereze, koma za Iye..chiweruzo chakufufuza kubweranso kwachiwiri kusanachitike'chi chikukhuzidwa ndi kubvomereza kwake[Yesu] kwakupereka moyo [ndi kufa] m'malo mwathu, osati kupereka kwa moyo wathu."



## A ELLEN G. WHITE ANALOSERA CHINYENGO CHA UMUNTHU'CHI

M'masomphenya opatsidwa kwa ine, Ndinaona ntchito ya mtundu wina ikuchitidwa ndi alaliki a za thanzi. Abusa athu amangoyang'ana, kuonerera osamvetsetsa kuti chikuchitika nchiyani, [ndipo ndi momwedi zinthu zikuchitikira lero]. Maziko a chikhulupiriro chathu, chomwe chinakhazikitsidwa ndi mapemphero osalekeza, kufufuza m'Malembo kosaneneka, chimanka chikugwetsedwa pansi, chiphunzitso kwa chiphunzitso. Chikhulupiriro chathu chinakhala chopanda maziko potsamirapo – chiphunzitso cha kachisi chinachotsedwa, cha chitetezero chinachotsedwanso…

Inu mukudabwa chifukwa chiyani ndiri wokhuzidwa pamene ndikuona ziphunzitso za chikhulupiriro chathu zikuchotsedwa? Ziphunzitso zosokeretsa zidzaphunzitsidwa m'malo mwa izi ndipo kudzakhala kobvuta kuzizindikira pokhapokhapo titadzakhala ozama m'chidziwitso chakulekanitsa mizimu. – Manuscript 46, May 18, 1904, "Maziko a Chikhulupiriro Chathu [The Foundation of Our faith]," zomwe zinalankhulidwa ku Berrien Springs, Michigan. Yang'anitsitsani kwa Yesu, [Upward Look], tsamba 152, ndime 4, 5.

Wowerenga aliyense wa Tabloid iyi ya chifupikitso cha bukhu, Our Evangelical Earthquake akulimbikitsidwa kugula lake kapena katoni yodzala ndi mabuku'wa momwe zalembedwa pamwambazi zikufotokozedwa mwakuya motsimikizidwa ndi maumboni oyenera. Lemberani ku Harvestime Books, Altamont, TN 37301. U.S.A.

TUMIZANI NDEMANGA NDI MAFUNSO ANU KU ADIRESI YOMWE MULI NAYO PAFUPI:

**RLMedia**

32 Ceres Str, Comptonville, Johannesburg, South Africa
www.rlmedia.co.za
+27(0)836254786